


Distributed by Parliamentary Monitoring Trust Zimbabwe
(www.pmtz.org/pmtzimbabwe@gmail.com/[@pmtzimbabwe@twitter](https://twitter.com/pmtzimbabwe))




MFUNDO ZIKHULU ZIKHULU

ZA

MAGANIZO A LAMULO LALIKHULU

LADZIKO LAZIMBABWE

(FEBRUARY, 2013)



CHICHEWA

MFUNDO ZIKHULU ZIKHULU

ZA

MAGANIZO A LAMULO LALIKHULU LADZIKO LAZIMBABWE

FEBRUARY 2013

Kutsegulila

Komiti yomwe ikutsogolela pakulembedwa kwa lamulo lalikulu ladziko ya Constitution Parliamentary Select Committee (COPAC) yatulusa chifupikiso chotsilizila chimenechi cha lamulo lalikulu ladziko la Zimbabwe cha chaka cha 2013, pofuna kuthandiza anthu adziko lino kuti amvetsetse zopezeka mukati mwa dongosolo ya lamulo limeneli. Dongosolo yonse yokwanila ili ndi matsamba zana, makumi asanu ndi awili (172). Komiti ya COPAC inapeza kuti ndikotheka kuti munthu omwe alibe nthawi yokwanila kuti awelenge dongosolo yonse, akhoza kuwelenga chifupikiso chimenechi kuti azindikile mwachidule zopezeka mudongosolo yonse.

Chiyambi

Chiyambi chimenechi chikulongosola ndi kuzindikira zosayenela zoyambisidwa ndi atsamunda, kulemekeza nsembe za amuna ndi akazi omwe anamenya nkondo yothetsa utsamunda. Chikuyan'ananso lamawa ndi ganizo lokhala ndi dziko la ulamulilo wokomela anthu onse pakudalila pa ulamulilo wa lamulo la dziko, kugwira nchito ndi mphamvu, kulemekeza ndi kukhalila paufulu wa chibadidwe ndi kumasuka, chigwilizano, zopezeka zachilengedwe ndikupeza chuma ku nzika zonse zadziko.

MUTU 1

Mfundo Za Chiyambi (Ndime 1-7)

- Zimbabwe ndi dziko lobadwa pa mfundo ndi maganizo otsatilawa:
- Zimbabwe ndi dziko limodzi lomvela ulamulilo umodzi wamugwilizano wa anthu amithundu wochokhela kumadela kwosiyana siyana, ndi dziko la ulamulilo wokwanilitsa ali yense, ndipo lokhala ndi ufulu wokwanila.
- Kuthi lamulo lalikhulu la dziko ndi lamulo loposa ena onse, ndipo chikhalidwe ndi muchitidwe uliwonse wolekana ndi lamulo lalikulu ladziko ili udzakhala osazindikilika.
- Lamulo lalikulu ladziko liyanjanisa anthu onse, kuphatikiza osunga malamulo, boma, utsogoleli wadziko, aphungu, nthambi zoweluzwa milandu ndi nthambi zina za boma.
- Mphamvu za lamulo lalikulu la dziko, kulemekeza malamulo, ufulu wa chibadidwe, kulekana kwa ziphemphezho, umunthu, kuyanjana kwa aliyense, kuyanjanisidwa pakati pa amuna ndi azimai ndi kulemekeza nkondo yomenyele ufulu wadziko.
- Ulamulilo wachilungamo wophatikiza zotsatilazi:
 - Ndale zozindikira zipani zosiyana-siyana;
 - Zisankho zochitika momasuka poyela ntahwi ndi nthawi;
 - Kupatsilana mphamvu zautsogoleli mumbuyo mwa zisankho;
 - Kulekana kwa mphamvu za ulamulilo pakati pa nthambi za utsogoleli wadziko, nyumba ya malamulo ndi nthambi yakuweluzidwa kwa milandu;
 - Kulemekeza anthu;
 - Kulimbikisa mugwilizano wadziko ndi bata;

- Kuzindikila ufulu wa magulu a anthu ochepa mudziko;
- Kugawidwa kwa zipatso zopezeka mudziko mofanana;
- Kufalitsa mphamvu za ulamulilo wa boma kumadela osiyana-siyana;
- Mwendela ya dziko, nyimbo yadziko, chizindikilo ndi chitsindikizo cha boma;
- Kuzindikila ulamulilo wa maboma azigawo, kumatauni akulu ndi maboma an'ono;
- Kuzindikila zilankhulo zazikulu zotsatilazi, Chichewa, Chibarwe, Chizungu, Kalanga, Koisan, Nambya, Ndau, Ndebele, Shangani, Chishona, Chinenedwe chapamanja (sign language), Sotho, Tonga, Tswana, Venda ndi Xhosa
- Kukhazikitsa kudziwika kwa lamulo lalikulu la dziko.

MUTU 2

Zolinga Za Boma (Ndime 8-34)

- Zimbabwe ndi dziko lokhala ndi zolinga zotsatilazi, zoyanjanisa boma, mukati ma mphamvu zopezeka muboma ili kuti:-
 - Pakhale ulamulilo wachilungamo kuptyolela ndi kukhazikitsa maudindo mopanda kukondela, kulimbana ndi ukatangale ndi kusagwilisidwa nchito bwino kwa mphamvu za nthambi zosiyana-siyana za boma ndi kuona kuti nthambi zonse za boma zili ndi ndalama zokwanila;
 - Kukwezelesa mugwilizano wadziko lonse, bata ndi mutendele;
 - Kuteteza ufulu wa chibadidwe ndi kumasulika kwa anthu;
 - Kutenga mfundo za malamulo akumayiko akunja zoteteza zofunila zadziko, zolemekeza malamulo adziko lonse lapansi, kukwezeletsa kukhalisana ndi mayiko ena mwabata ndi kuthetsa mikangano ndi mayiko ena a dziko lonse lapansi mwa bata;
 - Kupatsila mipata ya chitukuko cha dziko, kukwezeletsa nzika za dziko malinga ndi za chuma, ndi kupezela anthu zinchito zatsopano;
 - Kuona kuti dziko lili ndi chakudya chokwanila, kukwezeletsa chikkhalidwe cha anthu, chiyanjano pakati pa amuna ndi akazi ndi kukhala ndi mitundu yosiyana-siyana kuchokela munthambi zonse za boma;

- Kukwezeletsa zofuna za ana, achinyamata, okhalamba, olumala, anthu omwe anamenyela nkondo yomasula dziko, a nchito, mabanja ndi ukwati;
- Kupeleka mapunzilo a ulele kwa mwana aliyense a ku sukulu za pansi
- Kupeleka malo okhala, kupeleka zofunikila pa za moyo, chithandizo kwa osauka ndi kupeleka chithandizo cha zamalamulo ndi kuona kuti nzika zili ndi malo a zamasewela ofunikila;
- Kuteteza ndi kusunga luso la makono;
- Kukhazikitsa ngati lamulo la dziko migwilizano ndi malamulo a mayiko akunja.

MUTU 3

Zambadwe (Ndime 35-43)

- Unzika wa Zimbabwe upezeka kupyolela ndi kubadwila mudziko, ngati makolo anali nzika ndi kulembetsa.
- Nzika zonse zili ndi ufulu wopeza:
 - Chitetezo kuchokela ku boma;
 - Zipatso;
 - Zitupa zakubadwa ndi zina zitupa zoyenela kupelekedwa ndi boma.
- Anthu wolandila unzika kupyolela ndi anthu:
 - Wobadwa mudziko la Zimbabwe ndi amai kapena bambo womwe anali nzika ya dziko la Zimbabwe kapena kuti agogo anali nzika ya dziko la Zimbabwe ndi mbadwe kapena kupyolela makolo awo, kapena.
 - Womwe anabadwa kunja kwa dziko lino, ngati wina wa makolo ake anali nzika ya dziko la Zimbabwe ndi kukhala mu Zimbabwe koma akugwila nchito ya boma kunja kwa dziko la Zimbabwe kapena lina bungwe lokhudza nchito yapadziko lonse lapansi; kapena.
 - Womwe, popezeka mudziko la Zimbabwe ndi ana a zaka zosafika pa khumi ndi zisanu (15) ndiponso unzika wawo ndi makoklo sakudziwika;
 - Womwe anabwadwa mudziko la Zimbabwe lamulo limeneli lisinayambe kugwila nchito ndiponso wina wa makolo awo kapena makolo onse anali nzika ya dziko

lomwe likukhalila mubungwe la Southern African Development Community ndikukhala munthu okhala mudziko la Zimbabwe.

- Nzika zotengela unzika kupsoyolela kumakolo ndi anthu obadwa kunja kwa dziko la Zimbabwe kudzela kapena kwa amai kapena abambo emwe anali nzika ya dziko la Zimbabwe pa mubadwe kapena kutengela unzika kupsoyolela ku makolo ndi kuti chibadwe chawo chinalembesedwa mu Zimbabwe.
- Nzika zotengela unzika kupsoyolela ndi kulembetsa ndi anthu oti panthawi yolembetsa awapatsa chilolezo kukhala nzika za mu Zimbabwe.
- Unzika wa mayiko awili ndiwovomelezedwa kwa anthu obadwila mudziko la Zimbabwe kuyambila pano.
- Koma lamulo lokhazikitsidwa likhoza kuletsa unzika wa mayiko awili kwa iwo olandila unzika kupsoyolela makolo kapena kulembetsa.
- Unzika kupsoyolela ndi mbadwe ukhoza kuletsedwa ngati utapezeka mwa njira ya chinyengo, kunama, kapena kubisa mawu ofunikira.
- Unzika kupsoyolela ndi mbadwe ukhoza kuletsedwa ngati utapezeka mwa njira ya chinyengo, kunama, kapena kubisa mawu ofunikira kapena ngati pa nthawi ya nkhondo munthu wokhudzidwayo anali kuchita malonda ndi kapena kukambilana kapena kukhalilana kapena kuthandizila adani pa nthawi ya nkhondo.
- Unzika wa munthu aliyense siungalandidwe ngati munthuyo akatsala alibe unzika wozindikilika.
- Payenela kukhazikitsidwa bungwe la Citizenship and Immigration Board ndi nyumba ya malamulo kuti ligwile nkani za unzika ndi chilolezo chogwila nchito mudziko.

MUTU 4

Chigamulo Cha Ufulu (Ndime 44-87)

GAWO 1

Mfundo Zina Zapadela

- Munthu aliyense ndi boma ziyenela kutsatila ndikutetezeka ndi chigamulo cha ufulu.

GAWO 2

Ufulu Ndi Kumasuka

- Ufulu wa chibadidwe ndi kumasuka kuli monga:
 - Munthu aliyense ali ndi ufulu wokhala ndi moyo koma:
 - Lamulo likhoza kuloleza kuti munthu atemeledwe chilango cha imfa ngati akapha wina munthu dala;
 - Chilango cha imfa sichitha kutemeledwa kwa munthu wa mukazi kapena munthu wa zaka zosafika makumi awili ndi chimodzi (21years) pamene mulandu unagwidwa kapena munthu wa zaka zofika makumi asanu ndi awili (70yrs).
 - Ufulu wa mwana omwe asanabadwe uyanela kutetezedwa. Kuchotsa pathupi ndikoletsedwa ndi lamulo.
 - Munthu aliyense ali ndi ufulu kukhala womasuka ndipo sangathe :
 - Kutsekeledwa popanda chiweluzo kapena kupondeleza ufulu wake dala popanda chifukwa;
 - Kutsekeledwa mundende chifukwa cholephela kukwanilisa mfundo ina ili yonse.
 - Anthu womangidwa kapena kutsekeledwa ayenela:
 - Kudziwitsidwa chifukwa awamangila kapena kuwatsekela;
 - Kuloledwa kunena ndi mamuna kapena mukazi wake kapena wachibale kapena loya wake ndipo boma liyenela kulipila;
 - Kupatsidwa chilolezo chofunsila loya kapena dotolo wake wofuna iye nalipila yekha;
 - Kugwidwa mwachilungamo;
 - Ngati milandu wake usanayambe kuweluzidwa ayenela kumasulidwa popanda zifukwa zomukakamila ndipo momasuka;
 - Ayenela kuonekela kubwalo la milandu mukati ma maowala makumi anai ndi asanu ndi atatu(48 hrs);
 - Ali ndi ufulu wolimbana ndi lamulo lomwe amumangila kapena kumutsekela mubwalo la milandu;
 - Ali ndi ufulu wosayankha mafunso ndipo kuuzidwa za ufulu umenewu pa nthawi yomwe amutsekela;

- Sayenela kukakamizidwa kuulula chilli chonse kapena kubvomela milandu uli wonse;
- Ali ndi ufulu woyendeledwa ndi kulankhula ndi mamuna kapena mukazi wawo, kapena wachibale kapena womulangiza kapena wina aliyense;
- Ayenela kuweluzidwa mukati mwa nthawi yoyenela kupanda kutelo ayenela kumasulidwa popanda china chomukakamizila kapena zifukwa zofunikila.
- Munthu aliyense ali ndi ufulu kukweza dandaulo lake loti amumasule kukwalo la High Court ngati atamutsekela musatsatila malamulo kapena ngati pa nthawi yotsekeledwa sakudziwika komwe ali kumusunga.
- Munthu aliyense ali ndi ufulu wolandila malipilo ngati akamumanga ndikumutsekela dala popanda milandu kuchokela kwa iye yemwe wachitisa kuti amangidwe.
- Munthu aliyense ali ndi ufulu wachikhalile woti ayenela kulemekezedwa.
- Munthu aliyense ali ndi ufulu wotetezedwa kuphatikiza ufulu wokana kukhala mboni kapena kutengedwa ngati chifanizilo cha umboni.
- Palibe munthu yemwe ati azamuzunze kapena kugwidwa ndi nkhanza koma njila yosakomela munthu kapena njila yoyipisira kapena kumulanga.
- Palibe munthu yemwe adzatengedwe nkhati kapolo kapena wa nchito wosalipidwa kapena kugwila nchito yokakamizidwa.
- Anthu onse ndiwofanana pamaso pa malamulo ndipo munthu aliyense ali ndi ufulu kuti asagwidwe mwa njila yotsalidwa.
- Munthu ali yense ali ndi ufulu wa chinsinsi:
 - Kunyumba kwake, malo omwe ali mudzina lake ndipo malo ake sangalowedwe ndikufufuzidwa popanda chilolezo;
 - Ngipo atundu wake sangalandidwe;
 - Kuthi kunena kwake ndi munthu ali yense kukhala kwachinsinsi;
 - Mathenda ake asachulidwe poyela ndi ali yense popanda chilolezo chake.
- Munthu ali yense ali ndi ufulu kukumana ndi ali yense kapena kukhala mumodzi wagulu lili lonse ndipo sangamukhakamize:
 - Kuthi akhale nthambi yagulu lili lonse kapena
 - Kukala nawo mumusonkano uli wonse iye nasafuna.

- Munthu ali yense ali nawo ufulu wotsathila chikhalidwe chake ndipo sadzakhamukakamiza kulumbila ngathi chikhalidwe chakhe sichogwilizana ndimuchithidwe wothelo.
- Munthu ali yense ali ndi ufulu womasuka kunena chili chonse ndipo ufuluwo uphathikiza:
 - Ufulu waiwo olemba nkani;
 - Kutethezedwa kwa anthu ndi komwe anthola nkani apeza umboni wolembela nkani zili zonse.
 - Ufulu wokhazikitsa nchito kapena nyumba youlutsa nkani ingakhale wailesi kapena kanema pokapokapo ngathi athaloledwa malinga ndi lamulo loulutsa mau;

Koma ufulu woulutsa kapena kunena chili chonse uletsa kuyambitsa ziwawa, kunena mau achidani, kutukwana munthu, kapena kupondeleza ufulu wa munthu ali yense wachinsinsi.

- Nzika ili yonse kapena munthu wololedwa kukhala mudziko laZimbabwe ali ndi ufulu kupeza umboni kapena mau wofunikila omwe ali mumanja yanthambi ili yonse yaboma ngathi umboni kapena mauwo akhoza kuthandizila anthu wamba.
- Munthu ali yense ali ndi ufulu kulandila mau kapena umboni womwe uli mumanja mwamunthu ali yense ngathi mau wo kapena ali wofunikila kutetezela ufulu wawina munthu.
- Munthu ali yense ali ndi ufulu kunena chilankulidwe chili chonse chomwe angafune kapena kuchitha zinthu monga angafunile malinga ndi chikhalidwe chakhe.
- Munthu ali yense ali ndi ufulu kusanka nchito yomwe angafune kugwila, malonda ali onse malinga ndi malamulo amudziko laZimbabwe.
- Munthu ali yense ali ndi ufulu kugwidwa bwino panchito yakhe ndipo kulipilidwa malipilo okwanila.
- Munthu ali yense kupathulapo wogwila nchito munthambi yazachitetezo , ali ndi ufulu kuyambitsa gulu kapena kuyambitsa bungwe lomenyela ufulu wazaanchito, bungwe lomenyala ufulu waiyo wolemba ena zinchito kapena kukhala nawo paziwonetselo zamkwiyo kapena kunyanyala nchito ngathi ali ndi zifukwa.
- Ngathi munthu wamukazi ndi mwamuna ali kugwila nchito yofanana ayenela kulandila malipilo ofanana.
- Munthu ali yense ali ndi ufulu woyenda pali ponse, kulowa muZimbabwe, ndipo ali ndi ufulu kukhala ndi chipatso, ndipo ali ndi ufulu kuyendela malo ali wonse

muZimbabwe, kukhala malo ali onse muZimbabwe, kapena kuthulukha mudziko laZimbabwe.

➤ Nzika ili yonse ili ndi ufulu:

- Kuchititsa zisanko momasuka nthawi ndi nthawi;
- Kusankha monga angafunile momasuka;
- Kukhala nthambi yachipani chandale chili chonse;
- Kukhopa anthu kuthi aponye chisanko mumalo mwachipani chilli chonse mwomasuka mosakhakamizidwa;
- Kuponya vhoti ili yonse;
- Kusankidwa muchisanko chili chonse.

➤ Munthu ali yense ali ndi ufulu wolandila chiyanjano kumabwalo pankhani zanchito.

➤ Munthu ali yense ali ndi ufulu wopitha kubwalo lamilandu, kulandila chiweluzo chofunukila, kuweluzidwa mwachangu kubwalo lamilandu ndipo kuweluzidwa ndi munthu wosakondela kubwalo lokazikitsidwa ndi malamulo, ndipo ayenela kuimilidwa ndi loya wosanka yekha malinga ndi kukwanilitsa kulipila yekha.

➤ Munthu ali yense womangidwa ndi kuwombeledwa milandu ali ndi ufulu:

- Kutengedwa ngathi munthu wopanda milandu kufikana atha gwidwa ndi milandu mubwalo lamulandu;
- Kudziwitsidwa musanga zamulandu womwe ali kumumangila;
- Kupatsidwa nthawi yokwanila kukonzekela milandu wakhe;
- Kusanka loya womuimila womwe angafune;
- Kuimilidwa ndi loya womwe boma lamuthandizila nalo ngathi pamulandu wakhe pangakhale kusaweluzidwa bwino;
- Kuthi munthu akhale alipo ngathi ali kuweluzidwa;
- Kuthulutsa kapena kukana umboni uli wonse ndipo kukhana kuyanka mafunso;
- Kuthi munthu aweluzidwe muchilankulidwe chomwe angafune ndipo pakhale munthu womasulila kuthi amvetsetse;

- Kudandaula kubwalo lamilandu lapamwamba ngathi sakugwilizana ndi kugwidwa ndi milandu kapena kuthi ngathi Sali kugwilizana ndi chilango chomwe amuthemela.
- Munthu ali yense ali ndi ufulu kukhala ndikathundu kugulitsa kuthundu, koma pali malamulo olekhana ngathi ili nthaka yazaulimi.
- Kupathulapo nthaka yazaulimi, munthu ali yense ali ndi ufulu kuthi asalandidwe malo akhe:
- kulandidwa kuyenela kutsatila malamulo;
- kulandidwa ndi koyenela ngathi nthaka ikomela anthu ambili, kugwilitsidwa nchito kuteteza dziko, kuteteza nzika zambili ndi kukomela anthu wamba, ndi zina zotelo;
- lamulo liyenela kuthi polanda nthaka mwini wake apatsidwe nthawi yokwanila kuthi nthaka ikulandidwa ndipo kulandila malipilo pachilichonse chomwe chamangidwa panthaka yomweyo;
- lamulo lipatsa mwini wanthaka kuthi akweze nkhani yakhe yanthaka kubwalo ngathi pali mikangano kuthi pakhale kugamula, malinga ndi kulandidwa kwanthaka ndi malipilo omwe anga patsidwe.
- Munthu ali yense ali ndi ufulu kukhala ndi kathundu kupathikiza nthaka. Koma boma likoza kulanda malo azaulimi:
- kukhalitsa anthu kuthi alime;
- kukhalitsa anthu mwatsopano;
- kusamutsa anthu ndi kuwakhazikitsa pamalo ena atsopano;

Ndipo:

- palibe malipilo omwe athi achitidwe kupatyulapo zomanga manga zatsopano zomwe zili panthaka, kupathulapo ngathi nthaka yolandidwa ili mumanja mwa nzika yamudziko lino laZimbabwe, kapena ngathi nthaka ili pansi pamugwilizano pakhathi padziko lamwini wanthaka ndi dziko laZimbabwe, ndiye malipilo okwanila ayenela kupelekedwa;
- palibe munthu wokana kuthi nthaka ilandidwe pupsyolela bwalo lamilandu pokapokapo ngathi ali kufuna kuthi alandile malipilo azomanga manga panthakayo;
- munthu olandidwa nthaka sangakhanilile panthaka chifukwa nthaka ikulandidwa mwanjila yomupondeleza ufulu wake;

- Nthaka yazaulimi yomwe inalandidwa kuthi igawilidwe kwaiwo oaphanda nthakha yazaulimi lamulo lalikhulu ili lisanayambe kugwila nchito nthakayo iyenela kukhala mumanja mwaboma ndipo palibe malipilo omwe athi achithidwe pokapokapo ngathi malipilo ali kuchidwa chifukwa chazomanga manga zomwe zinamangidwa nthakayo isalandidwe.
- Panthawi yolanda nthaka yazaulimi mokakamiza kuthi anthu agawilidwe nthakayo, zotsathila ziyenela kuikidwa mumtima kupambana zina zonse ndipo izi ndi kuthi nzika zamu Zumbabwe zinalandidwa nthaka yazaulimi panthawi yaulumulilo waatsamunda ndi kuthi nzika zamu Zimbabwe zinamenyela nkondo kuthi nthaka ibwelele mumanja mwanzika zadziko ndipo kuthi akhale eni akhe nthakayo mwaufulu.
- Ulamulilo waatsamunda wakhale uli ndi udindo wolipila chili chonse choyenela kulipidwa panthaka yiolandidwa mokakamiza kuthi anthi asauka apeze nthaka yazaulimi.
- Munthu ali yense ali ndi ufulu:
 - kukhala pamalo abwino osamudwazika;
 - kuthi malo omwe ali onse athetezedwe kuchitila kuthi mabanja amutsogolo nawo apeze chogwila panthaka ili yonse;
- Nzika ili yonse ili ndi ufulu kulandila mapunzilo akusukulu yapansi ulele.
- Munthu ali yense ali ndi ufulu kuyambitsa kuyambitsa sukulu ndi kusamalila sukulu modzilipila payekha kuthi azipunzitsa maphunzilo koma sayenela kutsala ali yense kugwilitsa nchito chili chonse choletsedwa ndi lamulo lalikhulu ladziko.
- Nzika ili yonse yadziko ndi munthu woledwa kukhala mudziko laZimbabwe ali ndi ufulu wolandila chithandizo chazaumoyo kupathikiza mathenda odziwika kuthi nziwoipisisa kwambili ndi panthawi yochila mwana.
- Palibe munthu yemwe athi amukanile kuthi alandile chitandizo chamankwala panthawi yangozi kuchipatala chili chonse.
- Munthu ali yense ali ndi ufulu kulandila chakudya chokwanila chotetezekha, ndi madzi oyela abwino.
- Munthu ali yense wazaka khumi zisanu ndi zitatu (18) ali nawo ufulu woyambitsa banja lake wosakhakamizidwa.
- Mwamuna ndi mwamuna sangakwathilane ndiponso akazi akho akha sanga kwathilane, malinga ndi lamulo lalikhulu ladziko.

GAWO 3

UFULU WINA WAPADELA

- Munthu ali yense wamukazi ali nawo ufulu wolemekezedwa monga akhuchithila wamwamuna kupathikiza kulandila mipata yofanana munkani zandale, muchikhalidwe ndi zachuma.
- Azimai ali ndi ufulu wofanana ndi amuna pankani zakhulandila chuma chochekela kumakolo ndi kulele ana.
- Malamulo onse, zikhalidwe, muchitidwe wamakono, wopondeleza ufulu wamuzimai siudzalandilidwa ngathi lamulo.
- Mwana ali yense ali ndi ufulu:
 - wogwilidwa bwino malinga ndi lamulo, kupathikiza ufulu kumveseledwa;
 - kupatsidwa dzina ndipo kugwilitsa nchito ndina labanja;
 - kuthi akhale ndi chithupa chosonyeza zakubadwa kwake;
 - kukhala nthambi yabanja ndipo kuleledwa mubanja;
 - kukhala ndi chitetezo kuthi asagwilitsidwe nchito yosalingana naye khapena popanda malipilo ndi kugwilidwa;
 - kuthi asalembedwe ngathi wina wazigawenga kapena kumenya nkondo kapena kutenga mbali paziwawa zili zonse;
 - kuthi asamukhakamize kutenga nawo mbali pazandale;
 - kuthi asatsekeledwe kufikana pothi ndicho chinthu chomalizila chomwe chingachitike panthawi yomweyo.
- Anthu okhalamba amusinkhu wopambana makhumi asanu ndi awili ayenela:
 - kulandila chithandizo kuchokela kubanja ndi boma;
 - kulandila chithandizo chandalama kupsyolela chitandizo munthambi zambili yaboma.
- Anthu olumala ayenela:
 - kuthandizidwa kuthi azichithile chili chonse angafune;

- kuthandizidwa kuthi azikhala ndi mabanja awo ndipo kutenga mbali pachili chonse pakukhalitsana ngathi anthu, maphunzilo ndi masewelo;
- kutetezedwa kuthi pasapezeze wina wasagwilidwa bwino chifukwa chakulumala;
- Kupatsidwa mupata kulandila chithandizo chamankwala kuzipathala, chilangizo ndi kuthi akhale munthu wolandilikha.
- Omwe anamwenyela nkondo yopezela ufulu wadziko, onse omwe anatandizila munkondo yomenyela ufulu wadziko ndi onse omwe anamangidwa ndi kuteskeledwa chifukwa chanchito yomwe anagwila pnthawi yomwenyela ufulu wadziko ayenela kelemekezedwa ndi kulandila chitandizo pazonse angafune muumoyo wawo.

GAWO 4 Ndi 5

KWANILITSO NDI CHILETSO

- Munthu ali yense, akuziyimila iye kapena ali mumalo mwa wina munthu kapena ena anthu ali ndi ufulu wopita kubwalo la milandu kuti bwaloli likakamidze kukwanilitsidwa kwa ufulu wa anthu.
- Ufulu wofunikila ndi kumasulika kuyenela kukwanilitsidwa ndikuyan'anilanso ufulu wa ena anthu.
- Ufulu wa anthu ukhoza kuchepetsedwa ndi lamulo lozindikilidwa, lokazikitsidwa ndi nyumba yalamamulo ndiponso liyenela kukomela munthu ali yense.
- Palibe lamulo lomwe lingachepetse:
 - Ufulu wa umoyo pokapokapo ngathi pagamulo yakuti munthu aphedwe malinga ndi lamulo ladziko;
 - Ufulu wa ulemu wa munthu;
 - Ufulu wasazunzidwa kapena kubvutisidwa, kuchotsedwa ulemu wa umunthu ndi kulangidwa kosayenela;
 - Ufulu wasatengedwa ngathi kapolo;
 - Ufulu woweluzidwa ndi chilungamo;
 - Ufulu wodziwitsidwa komwe kuli munthu womangidwa.

- Panthawi yaziwawa, ufulu wachibadidwe ndi kumasulika, kusiya kwa zochulidwa pamwamba, zikhoza kuchepetsedwa ndi lamulo lolembidwa mulamulo lalikhulu la dziko.
- Kupondezedwa kwa ufulu pa nthawi yaziwawa ndi komangitsa, ndipo palibe munthu yemwe angatetezedwe ndi lamulo lili lonse kuthi asamangidwe.

MUTU 5

Utsogoleli Wa Pamwamba (Ndime 88-115)

GAWO 1

Mphamvu Zapamwamba

- Mphamvu zapamwamba zimachokela ku anthu ndiye ziyenela kugwilisidwa nchito malinga ndi lamulo lalikhulu la dziko.
- Mphamvu zapamwamba zili mumanja mwa mutsogoleli wa dziko ndiye amazigwilitsa nchito kudzela bungwe la nduna za boma malinga ndi kulamulila kwa lamulo la dziko.

GAWO 2

Utsogoleli Wa Pamwamba

- Mtsogoleli wadziko ndiyenso mtsogoleli wa boma ndi bwana wa asilikali.
- Kukwezeletsa, kuteteza, kutsata ndi kulemekeza undandanda wa lamulo ladziko;
- Kukwezeleza chigwilizano ndi bata mudziko;
- Kuzindikila ndi kulemekeza mfundo za nkondo yaufulu wa dziko;
- Kuona kuti pali kutetezedwa kwa ufulu wofunikila wa anthu, kumasulikha ndi kutsathila lamulo ladziko;
- Kulemekeza anthu a mitundu yosiyana-siyana a dziko la Zimbabwe.
- Munthu emwe ndi nzika kupsyolela mbadwe kapena kutengela kumakolo, yemwe analembetsa mukaundula wa mayina oponya mavoti, emwe ali ndi zaka

zofika makumi anai, wokhala mudziko la Zimbabwe akhoza kusankhidwa ngati mutsogoleli wadziko kapena wotsatila mutsogoleli wadziko.

- Munthu yemwe akufuna kusankhidwa kukhala mutsogoleli wadziko ayenela kusankha anthu awili omwe adzakhala naye limodzi pachisankho chofuna mutsogoleli wadziko.
- Munthu wosakondwela akhoza kutsutsana ndi ubwino kapena zotuluka pa chisankho chofuna mutsogoleli wa dziko kapena wotsatila mutsogoleli wadziko kubwalo la milandu yokhudza za lamulo lalikhulu la dziko. Bwalo limeneli liyenela kukhazikitsa nkani imeneyi mukati mwa masiku khumi ndi anai (14days).
- Nthawi yokhala pa nchito ya mutsogoleli wadziko ndi mphindi ziwili za zaka zisanu pampindi imodzi.
- Mutsogoleli wa dziko kapena wotsatila mutsogoleli wadziko akhoza kusiya nchito yakhe ngati akufuna.
- Mutsogoleli wadziko kapena wotsatila mutsogoleli wadziko akhoza kuchotsedwa pa nchito ngati:
 - Atachita zosayenela;
 - Atalephela kubvomeleza, kusunga kapena kuteteza lamulo lalikhulu la dziko;
 - Atatyola lamulo lalikhulu la dziko mosa samala;
 - Atalephela kukwanilitsa nchito yakhe chifukwa chodwala kapena kusokonezeka bongo.
- Mutsogoleli wadziko sangayimbidwe milandu mubwalo lamilandu pa nkani ili yonse yomwe kufikhana pa nthawi yosiya nchito ya mutsogoleli wadziko. Pamalamulo a dziko, chilungamo ndi njira yoziteteza.
- Ngathi mutsogoleli wadziko atamwalila, kusiya nchito kapena atachotsedwa nchito, wotsathila mutsogoleli wadziko amatenga nchito yautsogoleli wadziko kufikana pa nthawi yonse yotsala yomwe mutsogoleli wadziko analikuyenela kugwila nchito;

GAWO 3

Nduna Za Woma, Wotsathila Nduna Za Boma Ndi Bungwe La Nduna Zaboma.

- Mutsogoleli wa dziko, ayenela akuganizila kakhaliidwe ka anthu onse kumadela a dziko ndi kuyanjanitsa pakathi pa amuna ndi akazi, adzasankha ndikukhazikitsa nduna za boma ndi wotsatila nduna za boma pakati pa aphungu anyumba yalamamulo. Akhozanso kusankha zina nduna zosapithilila zisanu kuchokela kunja kwa nyumba yalamamulo malinga ndi luso lawo ndi kudziwa zanchito.
- Bungwe la nduna za boma ndilomwe lili ndi udindo wopititsa mutsogolo nchito za boma, kuchita nchito za boma munyumba ya malamulo, kukonza, kuyambitsa ndikukhazikitsa malamulo ndi kuweluzwa mutsogoleli wadziko.

GAWO 5

Loya Wa Boma

- Tsopano pali loya wa boma yemwe nchito yake ndiyolangiza mutsogoleli wadziko ndi bungwe la nduna za boma pa nkani za malamulo ndipo amagwila nchito yake pachifunilo cha mutsogoleli wa dziko.
- Nkani zonse zakuyimbidwa milandu tsopano zidzalongosoledwa ndi bungwe la National Prosecuting Authority, lotsogoledwa ndi Prosecutor- General.

MUTU 6

KAKONZEDWE KA MALAMULO (Ndime 116-117)

GAWO 1

Mphamvu Zokonza Malamulo

- Bungwe lokonza malamulo likuphatikiza nyumba ya malamulo ndi mutsogoleli wadziko.
- Mphamvu zokonza malamulo adziko laZimbabwe zichokela ku anthu ndiye:
 - Kupatsila mphamvu kunyumba yalamamulo ndi mutsogoleli wa dziko zosintha lamulo lalikhulu la dziko;
 - Kukonza malamulo okhudza za bata, ulamulilo ndi ulamulilo wabwino;
 - Kupatsila mphamvu zokonza malamulo kulina bungwe kapena zina mphamvu.

GAWO 2

Nyumba Ya Malamulo

- Nyumba yalamamulo:
- Ili ndi nyumba ya Senate ndi National Assembly.
- Iyenela kuteteza lamulo lalikhulu la dziko ndi kukwezeleza ulamulilo wokomela anthu onse;
- Ili ndi mphamvu zochita kuti lamulo lalikulu ladziko litsatidwe.
- Mabungwe onse a boma akuyankha ndi kuvomela ku nyumba yalamamulo.

GAWO 3

Nyumba Ya Senate

- Nyumba ya Senate ili ndi aphungu makumi asanu ndi atatu (80 Senators) komwe:
- Asanu ndi mumodzi (6) akusankhidwa kuchokela kuchigawo chimodzi pa njira yoyan'ana unyinjira wa mavoti oponyedwa;
- Khumi ndi asanu ndi mumodzi (16) akhale mfumu, ziwili zakhe zimasankhidwa ndi bungwe la mfumu la dziko lonse zochokela chili chonse kupathulapo matauni a Baulawayo ndi Harare;
- Mfumu ziwili zidzakhala mutsogoleli ndi wachiwili wa bungwe la National Council of Chiefs;
- Mfumu ziwili zisankhidwa kuthi ziyimile anthu olumala.
- Amphungu a nyumba ya Senate osankhidwa pa njira yakuchulukha kwa mavhoti oponyedwa ayenela kusankhidwa kuchokhela kuchipani malinga ndi mavoti oponyedwa ku anthu woyimila zipani zandale kuchigawo chili chonse pa chisankho cha aphungu a nyumba ya National Assembly, anthu woyimila zipani zawo amenewa akuyimikidwa pa munda ndanda amuna ndikudzabwela muzimai, mundandanda uliwonse uyenela kuyamba ndi muzimai.
- Mphungu wa nyumba ya Senate ayenela kukhala munthu wopezeka dzina lake mu kaundula wa mayina a anthu oponya mavoti ndikukhala wazaka makumi anai(40years)zobadwa , mphungu woyimila mfumu ayenela akhale mfumu; phungu wa nyumba ya Senate woyimila anthu wolumala ayenela kukhala munthu wolumala.

- Munthu atsaletsedwa kuti asankhidwe ngati mphungu wa nyumba ya Senate ngathi ataletseda kuponya vothi kapena munthuyo anasiya mpando wauphungu munyumba yalamulo mukathi mwa zaka zisanu kutsathila chisankho atapezeka ndi milandu, kapena munthuyu ndi mphungu wa nyumba yalamulo chakale.
- Mutsogoleli wa nyumba ya Senate ndi wotsatila ayenela kutsogolela nyumba ya Senate.

GAWO 4

Nyumba Ya National Assembly

- Nyumba ya National Assembly imakhala ndi:
 - Aphungu mazana awili ndi khumi osankhidwa kupsyolelal ndi chisankho cholemekeza chinsinsi kuchokela kumadela mazana awili ndi khumi;ndi
 - Pa zigawo ziwili zakugwila nchito kwa nyumba yalamulo mbuyo moyamba kugwila nchito kwa lamulo lalikhulu ili, azimai makumi asanu ndi khumi (60), adzawonjezedwa asanu ndimumodzi kuchokela kuchigawo chili chonse chadziko, adzasankhidwa kupyolela ndi kuchuluka kwamavhoti oponyeledwa oyimila chipani chili chonse cha ndale pachisankho chadziko muzigawo zawo.
- Zonse zofunikira kuti munthu akhale phungu munyumba yaseneti zigwilanso muchigawo chino kupathula malile a zaka zobadwa zomwe ziyenela kukhala makumi awili ndi chimodzi (21yrs).
- Muneneli ndi wachiwili wakhe munyumba yalamulo ndi omwe otsogolela nchito munyumba ya National Assembly.

GAWO 5

NTHAWI YA APHUNGU A NYUMBA YAMALAMULO

- Zifukwa zosiila nchito mphungu wa nyumba ya malamulo ndi zomasulidwa mulamulo lalikhulu ladziko ndipo zikuphatikiza kusiya chipani, kusiya nchito, kupekekha ndi mulandu ndi kupezerkha ndi mulandu wazakhubela chisankho.

GAWO 6

Mphamvu Za Nyumba Yamalamulo

- Nyumba yalamamulo ili ndi mphamvu zoyambitsa, kukonzekela, kuganizila kapena kukana lamulo lilo lonse lomwe lingabwele kunyumba yamalalo.
- Mphamvu za nyumba yalamamulo zokonzala malamulo zimaphezeka kudzala malamulo okazikitsidwa munyumba yalamamulo.
- Mfundo zotsatidwa polandila maganizo munyumba yalamamulo ndizomasulidwa mundime yachisanu.
- Nyumba yalamamulo ikhoza kuphatsila mphamvu zakakonsedwe kamalamulo kubungwe lili lonse lokhazikitsidwa ndi malamulo.

GAWO 7

Kayendesedwe Ka Nchito Munyumba Ya Malamulo

- Mutsogoleli wa nyumba yalamamulo ndi muneneli wanyumbayi ndiponso mutsogoleli wanyumba ya seneti ndiye mutsogoleli wanyumbayi.
- Mulembi wanyumba yalamamulo adzakhala mutsogoleli wazinchito zonse zamunyumba yalamamulo ndipo adzakhala paudio uwu kwazakha zisanu ndi umodzi zongowonjezwdwa kamodzi.

GAWO 8

Nthawi yakugwila nchito, kuyimisidwa kwa nchito yanyumba yalamamulo ndi misonkano ya nyumba yalamamulo.

- Nyumba ya malamulo imagwila nchito zaka zisanu ndiye imayimisidwa nchito tsiku limodzi popita kukaponya mavoti pachisankho chotsatila.
- Nyumba yalamamulo ikhoza kusankha kuti iyimisidwe nchito ndiye pamenepa mutsogoleli wadziko ayenela kuyimisa nchito nyumbayi.
- Ngati nyumba yalamamulo ikukana popanda chifukwa kukhazikitsa lamulo lapadela, mutsogoleli eadziko akhoza kuyimisa nchito nyumbayi, koma kuyimisidwa nchito kwanyumbayi kukhozanso kukanidwa mubwalo la Constitutional Court ngati wina wa aphungu anyumba yalamamulo atalembela kubwaloli napempha kuti zimenezi zichitike.

- Ngati zonse zikuyenda bwino ,mutsogoleli wadziko ayenela kuyitanila chisankho mukati ma masiku makumi atatu tsiku lomazilila likugwila nchito kwa nyumbayi lisanafike.
- Chisankho chofuna atsogoleli chochitidwa chifukwa chakuyimisidwa nchito kwa nyumba yalamamulo nthawi yake isanafike, chiyenela kuchitidwa mukati ma masiku makumi asanu ndi anai mmbuyo moyimisa nchito yanyumbayi.
- Mutsogoleli wa dziko ayenela kulankhulana ndi kugwilizana ndi bungwe la Electoral Commission pofuna kukhazikitsa masiku a chisankho chofuna atsogoleli chilli chonse.
- Musonkhano woyamba wa nyumba yalamamulo umachitidwa mukati ma masiku makumi asanu ndi anai mmbuyo makuyamba nchito kwa mutsogoleli wa dziko.
- Nyumba yalamamulo ili yonse iyenela kukhazikitsa nthawi yamisonkano ndi nthawi zopuma. Koma, mutsogoleli wadziko akhoza kuyitana aphungu anyumba yalamamulo nthawi iliyonse kuti agwile nchito yofunikila pa nthawi ili yonse. Misonkano yanyumba yalamamulo siyiyenela kulekana ndi masiku optilila zana ndi makumi asanu ndi atatu (180).
- Azitsogoleli a makomiti ndi ena wotsogolela magulu a amphungu a nyumba yalamamulo sangayimbidwe milandu uliwonse wochokela pa zomwe amanena munyumba yalamamulo.
- Nzika zonse zadziko zili ndi ufulu wokweza madandaulo azo kunyumba yalamamulo.

MUTU 7

ZISANKO (Ndime 155-161)

GAWO 1

KAYENDESEDWE KA MASANKO

- Zisanku ziyenela kuchitidwa mwabata, momasuka ndi chilungamo, ndipo ziyenela kuchitidwa molemekeza chinsinsi ndipopayenela kukhala mipata kuti anthu onse omwe akhoza kuponya chisanku apatsidwa mupata wochita zimenezi.
- Bungwe loyendesa masanku liyenela kuona khuti:
 - kuponya chisanku chachitika molondoleka, mwachilungamo, motetezeka ndi poyela;

- zotsathila zachisanko ziyenela kulengezedwa musanga musanga chisanko chithata;
- ziwawa ndi kusokoneza kuli konse kuyenela kuletsedwa;
- zonse zogwilitsidwa nchito pazisanko zasungidwa bwino;
- Boma liyenela kupsolela ndi malamulo nd njila zina, kuona kuthi:-
- anthu onse oyenela kuponya voti ochulidwa mundime yachinayi ndi anthu olembetsa kuponya chisanko.
- kuthi ali yense woyenela kuponya chisanko alandila mupatha wothelo;
- kuthi zipani zandale ndi anthu onse othenga nawo mbali pazisanko alandila utenga wofunikila;
- kuthi zipani zandale ndi anthu othenga mbali pazisanko apeza mipata yofanana kumapepala olemba nkani ndi mawailesi ndi kanema zaboma ndi zodziyimila pazokha;
- mikangano yonse yazandale yatetsedwa mwachangu.
- Lamulo lachisanko liyenela kuona kuthi:
- pali kudulidwa kwamalo amwe akuimilidwa pazisanko;
- kuthi onse oponya chisanko awalembetsa;
- payenela kukhala ndi njila yotsathidwa pochithitsa zisanko mogwilizana;
- kuthi pakhale njila yothi chipani chomwe chalandila mavhoti ochuluka mudela lili lonse apeze mupatha wosanka anthu akhalila malo omwe alibe anthu munyumba yamalamulo;
- kuthi pakhale phungu wanyumba yapamwamba woimila wolumala.
- kuthi anthu afuna kusankidwa pachisanko alembetse maina awo matsiku khumi ndi anai tsiku lachisanko lithachulidwa ndipo panso pamasiku makumi atatu tsiku loponya chisanko lisanafike.
- Palibe kusinthidwa kwalamulo lachisanko kapena lamulo lili lonse lazachisanko lotsathila popanda kuimilidwa ndi bungwe la Electoral Commission;
- Ngathi chisanko chikaitanidwa kusintha kwalamulo lili lonse lakhaendesedwe kachisanko sikhatha kusintha chonse malinga ndi kagwilidwe kachisankochi.

GAWO 2

NTHAWI YOCHITA ZISANKO

- Chisanko chanthambi zonse chiyenela kuchitika:
- sipanaduse matsiku makhumi atatu nyumba yamalamulo ithaimitsidwa nchito kapena nthawi yogwila nchito yanyumba yamalamulo ithatha; kapena
- mukathi mwamasiku makhumi asnu ndi anayi nyumba yamalamulo itayimitsidwa nchito; kapena
- matsiku makumi asanu ndi anayi nyumba yamalamulo itayimitsidwa nchito mumbuyo mwakudandaula kuthi nyumbayo ilibenso chidalilo ndiboma;
- Chisanko chamakonsolo chiyenela kuchithidwa nthawi imodzi ndi chisanko cha mutsogoleli wadziko ndi aphungu.
- Chisanko chamubwelezo chiyenela kuchithika mukathi mwamatsiku makumi asanu ndi anayi pambuyo pothi udindo walengezedwa kuthi ulibe munthu kupathulapo kuthi udindowo wakhala ulibe munthu mwezi isanu nthawi yachisanko isanafike kulephela kuthelo udindo womwewo udzakhala ulibe munthu kufikila chisanko chanthambi zonse.
- Mipando yonse yoyenela kusankidwa munthu malinga ndi lamulo lalikhulu ladziko iyenela kuthengedwa ndi munthu mukhathi mwa masiku makumi asanu ndi anayi.

GAWO 3

Kudulidwa Kwamalile A Malo A Zisanko

- Kuthandizila zisanko zaaphungu munyumba yamalamulo, bungwe la Electoral Commission liyenela kudula madela osiyana asiyana kukhala mazana mazana awili ndi limodzi (210) pazisanko zamakonsolo liyenela kudula malo kukhala mawadhi malinga ndi malamulo.
- Kudula malile amalo azisanko kuyenela kuchithika kamodzi mukathi mwazaka kumi mofulumila chiwelengelo chaanthu chithachithika.
- Kudulidwa kwamnalile panso pamwezi isanu ndi umodzi nthawi yachisanko isanafike sikuthengedwa ngathi kholingana ndi chisanko chanthawi yiomweyo.

- Payenela kukhala dongosolo yakadulidwe kamalile amalo achisanko ndipo kupelekhedwa kunyumba yamalamulo ndi mutsogoleli wadziko ndipo ngathi pali zina zofunikhila ziyenela kuchulidwa ndibungwe lazisanko.
- Mutsogoleli wadziko ayenela kupelekhwa dongosolo ndimaina amalile amalo odulidwa, kulembetsa matsiku ndi kudziwitsa mawadhi omwe athi akhale okazokitsidwa ndi bungwe lazisanko.

MUTU 8

KUWELUZA NDI MABWALO A MILANDU

(162-193)

GAWO 1

Nchito ya mabwalo amilandu

- Mphamvu zoweluza milandu zimachokela ku anthu a dziko la Zimbabwe ndipo zaikidwa mumanja mwa mabwalo amilandu kuphatikiza bwalo la Constitutional Court, Supreme Court, High Court, Labour Court, Administrative Court, magistrates courts, customary law court, ndi ena mabwalo okazikitsidwa malinga ndi malamulo adziko.
- Bungwe la aweluza milandu lipathikiza Chief Justice, Deputy Chief Justice, Judge President, ndi ena oweluza milandu. Chief Justice ndiye mutsogoleli wabungwe laoweluza milandu.
- Mabwalo a milandu ayenela kukhala oziyimila okha, osatenga maganizo kuchokela kwamunthu aliyense ndipo okhala ndi mphamvu.
- Boma liyenela kuteteza mabwalo amilandu.
- Wogwila nchito zoweluza milandu ayenela kutsogoleledwa ndi zotsatila izi:
 - Kuwona kuthi chilungamo chikuchitidwa kwa anthu onse;
 - Kuwona kuthi chiweluzo sichichedwa;
 - Kuona kuti nchito ya bwalo la milandu ndiyofunikira poteteza ufulu, kumasulika kwawo ndi ulamulilo wotsatila malamulo adziko;

- Wogwila nchito kumabwalo amilandu sayenela kuloweleda ku zandale kapena kulandila chiwongola dzanja, koma ku kwezeletsa nchito zawo ndikukhala akudziwa zochitika munkani za malamulo nthawi ndi nthawi.
- Bwalo la Constitutional Court ndi bwalo lapamwamba pa nkani zonse zokhudza nkani za lamulo lalikhulu ladziko.
- Bwalo la Supreme Court ndi bwalo lapamwamba lozenga milandu yonse, ndipo bwalo lodandaulila milandu, kupathula nkani zokhudza malamulo zomwe bwalo la Constitutional Court ndi lomwe lili ndi mphamvu zolamulila
- Bwalo la High Court ndi bwalo lapamwamba loweluka ndi kumvela nkani ndi madandaulo onse ochekhela kumabwalo aan'ono ndipo liyan'anila nchito zaena mabwalo aan'ono..
- Bwalo la Labour Court ndi bwalo lolongosola nkani zonse za kagwilidwe kazinchito.
- Mphamvu, kukhazikitsidwa ndi wozenga milandu kumabwalo a magistrate, ndi mabwalo a nkani za lamulo lakakhalidwe ka anthu zikhoza kupezeka pa lamulo la dziko.

GAWO 2

Kusankidwa ndi nthawi yokhala panchito ya wogwila nchito ya oweluza.

- Zofunikira ku anthu omwe akufuna nchito ya woweluzanga milandu kumabwalo onse, nthawi yawo yokhala pa nchito ndi njira yogwilitsidwa nchito kupeza anthuwa ndikuchotsedwa kwawo pa nchito, zonse zimenezi zili mulamulo lalikulu la dziko.
- Munthu amayenela kusankhidwa ngathi woweluza milandu ngathi atakhala loya kwa zaka zisanu ndi ziwili (7yrs), koma wofuna kukhala woweluza milandu kubwalo la Supreme Court akhale munthu yemwe athagwila nchito ngathi loya kwa zaka khumi, zakha khumi ndi ziwili munthu yemwe akufuna kuweluzira milandu kubwalo la Supreme Court.
- Woweluza milanduwa adzakhala akusankhidwa motsathila njira izi.
 - Uthenga wofalisidwa kumapepala kapena kwina kwake;
 - Kuyitana mutsogoleli wa dziko ndi anthu kuti asankhe anthu omwe angasankhidwe kutenga nchito zimenezi;
 - Kukhazikitsa mayeso abungwe losankha anthu;

- Kulemba maina aanthu atatu omwe adzatenge mmodzi kulowa nchito;
- Kupeleka mayinawa ku mutsogoleli wadziko.
- Woweluza milandu kubwalo la Constitutional Court onse ayenela kukhala wa zaka zofunikila posiya nchito kupita kukapuma, amapatsidwa zaka khumi ndi zisanu(15years). Woweluza milandu kubwalo la Supreme Court ndi la High Court amakhala pa nchito mphaka atafikisa zaka makumi asanu ndi awili (70years) zobadwa ali panchito ndiye sadzapitilila.
- Woweluza milandu amachotsedwa pa nchito ndi zifukwa zotsatila izi:
- Kulephela kugwila nchito yake chifukwa cha kudwala misala kapena chili chonse pathupi lake;
- Akulephela kukwanisila zofunika pogwila nchito yake;
- Khalidwe loyipa.
- Woweluza milandu amachotsedwa pa nchito ngathi kupsyolela zonena zabungwe lomwe linali kufufuza nkani yokhazikitsidwa ndi mutsogoleli wa dziko, ndipo bungwe limeneli liyenela kukhala ndi anthu atatu kapena kupambana.
- Mutsogoleli wadziko ayenela kuchitako kanthu malinga ndi ganizo la bungwe loweluza.

GAWO 3

Bungwe la Judicial Service Commission

- Nthambi ya zakuweluzidwa kwa milandu idzakhala ikutsogoledwa ndi bungwe la Judicial Service Commission ndipo litsogololedwa ndi Chief Justice.
- Zonse zofunikila zokwanila zikupezeka mulamulo lalikulu la dziko.
- Nchito zakhe zikuphatikiza:
 - Kulangiza mutsogoleli wadziko pa nkani zokhudza zakuweluzidwa kwa milandu ndi utsogoleli wa chilungamo;
 - Kukwezeletsa ufulu ndi ubwino wa nchito zakuweluzidwa kwa milandu ndi kayendesedwe ka nchito zotsogolela chilungamo;
 - Kukhazikitsa mfundo zokhudza zakuweluzidwa kwa milandu.

- Bungwe limeneli liyenela kugwila nchito yakhe mwa njila yachilungamo.

MUTU 9

MFUNDO ZAKAYENDESEDWE KA NCHITO ZA BOMA NDI UTSOGOLELI (Ndime 194-198)

Mutu uwu uli kutulusa poyela mfundo zotsogolela ndi kayendesedwe ka nchito za boma. Mfundo zimenezi zikuphatikiza nthambi za boma, makonsolo, makampani a boma ndi anthu omwe ali ndi mipando kumabungwe ndi makampani amwewa.

1. Kufunikila ndi Mfundo

- Pautsogoleli wonse wa nchito za boma, zotsatilazi ziyenela kuyan'anidwa bwino nthawi zonse:
- Kufunikila kwa ulamulilo wokomela munthu aliynse kopezeka mulamulo lalikhulu limeneli;
- Luso logwila nchito ndi mukhalidwe wofunikila;
- Mwachangu ndi kusamalila;
- Mosakondela kuli konse ndi kuyanjana;
- Kuyankha ndi kukhazikitsa zofuna za anthu mofulumila;
- Kufikika, chilungamo, utsogoleli wofunikhila womwe ukudza nkani za chitukuko;
- Kuloweleda mu nkani zakukonzedwa kwa ndondomeko zotsogolela kayendesedwe ka nchito;
- Ndondomeko zotsogolela nchito zokwezeletsa utsogoleli wa wogwila nchito popezela anthu zinchito zatsopano, kupunzitsidwa ndi kupititsa mutsogolo zodalila pa luso, anthuwo ayenela kukhala wokwanilitsa zonse zofunikila;
- Kuyanjana pakathi pa amuna ndi azimai ndi anthu olumala. (Ndime 194).

2 Makampani Ndi Mabungwe Oyendetsedwa Ndi Boma

- Makampani ndi mabungwe oyendetsedwa ndi boma ayenela kugwila nchito bwino ndikukwanilitsa za kachitidwe wachilungamo.

- Njila zogula nazo zinthu ziyenela kukhala zachiyelo ndi zolungama (gawo195).

3 Atsogoleli ndi Ogwila Nchito Za Boma

Atsogoleli ndi anchito a boma amagwila nchito yawo mokomela nanthu. Kachitidwe kawo kayenela kugwilizana ndi mfundo za lamulo ladziko. Ayenela kulemekeza anthu, kuwatumikila, osati kuwalamulila.

4 Atsogoleli A Makampani

Nthawi yokhala pa nchito ya atsogoleli wa makampani ndi mabungwe oyendetsedwa ndi boma iyenela kugamulidwa ndi lamulo.

5 Kupatsila mphamvu ku mfundo za utsogoleli wa zinchito

Padzakhazikidwa lamulo lotamanda zotsatila izi:

- Kulengezedwa poyela kwa zonse zomwe atsogoleli ndi anchito aboma angakhale nazo;
- Zakakhalidwe ndi kuzigwila bwino;
- Kukhazikitsa kakhalidwe koyenela ka ulamulilo wabwino kumakampani ndi mabungwe otsogoledwa ndi boma.

MUTU 10

Nchito za boma (Ndime 194-205)

1 Nchito za Boma

- Nthambi za bungwe la Civil Service ndi anthu olembedwa nchito ndi boma.
- Omwe akulephela kulowa mu bungwe la Civil Service ndi a polisi, asilikali, osunga akayidi kundende, wogwila nchito zakuweluzidwa kwa milandu ndi wogwila nchito kunyumba ya malamulo.
- Pogwila nchito zawo, anchito a boma amayembekezedwa kuthi:
 - Atsatile lamulo lalikhulu la dziko;
 - Asalandile zakunja kwa lamulo;
 - Sayenela kukondela chipani chili chonse cha ndale;

- Kulemekeza ufulu ndi kumasulika kwa anthu.
- 2 Olembedwa nchito ndibungwe la Civil Service sayenela kukhala ndi mipando kuzipani za ndale koma kuthi akhalile chapakati, osathi pambuyo pachipani cha ndale chili chonse.

3 Bungwe La Civil Service Commission

- Bungwe la Civil Service lidzatsogoledwa ndi bungwe la Civil Service Commission.
- Nthambi za bungwe la Civil Service Commission ziyenela kukhala anthu opunzila kuti a khale atsogoleli ndi nthambi za Bungweli, ndipo akusankhidwa ndi mutsogoleli wa boma.
- Nchito za bungwe ili liphatikiza kulemba anthu zinchito, kutsogolela kayendesedwe ka nchito, kukhazikitsa malipilo, zokudza malamulo, ndikufufuza za madandaulo a nchito a boma. Bungwe limeneli limalangizaa boma pa nkani zokhudza bungwe la Civil Service.
- Pa nkani ya malipilo ndi kagwilidwe ka nchito zawo, anchito a bomawa ali ndi ufulu wokambilana ndi boma. ali pabungwe lawo.

3 Akazembe

Akazembe adzasankhidwa ndi mutsogoleli wadziko, ndiye amagwila nchito yawo momvela iye.

4 Alembi Anthambi Zaboma

- Alembi anthambi zaboma adzasankhidwa ndi mutsogoleli wadziko mokambilana ndi bungwe la Public Service Commission
- Amakhala pa nchito zawo kwa zaka zisanu (5yrs) ndikupitiliza zina zaka zisanu ngathi akudziwa ndi akugwila nchito yawo bwino.

MUTU 11

Nthambi Za Chitetezo (206-210)

GAWO 1

1 Kayimidwe ka mabungwe a chitetezo

- Mabungwe a chitetezo akuphatikizapo a silikhali, a polisi, Ndende za dziko, a intelligence ndi bungwe lililonse lachitetezo chololedwa pa lamulo la dziko.

- Mabungwe amenewa ali ndi udindo woyan'anila za chitetezo ndiye nchito imeneyi iyenela kuchitidwa motsathila lamulo lalikulu ladziko ndi kulemekeza ufulu wa anthu ndi kumasulika kwa nzika zonse.
- Ayenela kukwezeletsa ulamulilo wa lamulo lali ladziko.

2 Nthambi za mabungwe a chitetezo

- Pogwila nchito zawo nthambi za mabungwe a chitetezo ayenela kuchita zotsatilazi:
 - Kutsatila lamulo lalikulu ladziko;
 - Sayenela kukhala anthu okhala ndi kuzipani za ndale;
 - Sayenela kukondela pa nkani za ndale;
 - Ayenela kulemekeza ufulu wofunikila ndi kumasulika kwa nzika zonse za boma.
- Sayenela kugwila nchito kumalo okhalila anthu omwe sakugwila nchito za usilikali, kusiya kwa nthawi zawawa.

3 Bungwe National Security Council

- Kudzakhala bungwe la National Security Council lomwe nchito yake ndiyokhazikitsa ndondomeko yoyenela ya chitetezo cha dziko.
- Lidzakhazikitsidwa ndi mutsogoleli wadziko, wotsatila mutsogoleli wadziko ndi zina nthambi malinga ndi zofuna za lamulo ladziko.

4 Madandaulo

Madandaulo ku nthambi za mabungwe a chitetezo adzalongosoledwa kudzela kunjila zosalowezeza mabungwe a chitetezo.

GAWO 2

Asilikali (Ndime 211-218)

1 Kayimidwe

- Asilikhali akuphatikiza asilikali a nkondo yapansi ndi yamulenga lenga. Zina nthambi zikhoza kukhazikitsidwa malinga ndi lamulo lalikhulu ladziko. Ayenela kukhalila pa izi:
 - Kukhala ndi nthambi zochokela kumadela onse adziko;

- Kukhalila pambuyo ndi kukonda dziko;
- Wopunzila ndi kudziwa nchito yawo;
- Wosakondela mbali iliyense;
- Kumvetsela ku ulamulilo wa anthu womwe osakhala asilikali;
- Wolemekezeka.

2 **Kutumizidwa kwa Asilikali kunkondo**

- Kutumizidwa kwa asilikali kupita ku nkondo ndi udindo wa mtsogoleli wadziko, yemwe ndi bwana wamkulu wa asilikali:
 - Poteteza dziko;
 - Kusunga kukhazikika kwa dziko;
 - Kukhalila mmbuyo mphamvu za mabungwe omwe sali achisilikali pakakhala ziwawa;
 - Kupita kunja kwa dziko la Zimbabwe pofuna kuteteza zofuna za dziko kapena kukwanilitsa zamabungwe a padziko lonse lapansi.
- Kutumizidwa kwa asilikali kuyenela kubvomelezedwa ndi nyumba yamalamulo, kupanda kutelo ganizo ili liyenela kuikidwa pambali.

3 **Atsogoleli a za nkondo**

- Atsogoleli a asilikazi:
 - Atsogoleli amasankhidwa ndi mtsogoleli wadziko atasinthana maganizo ndi nduna yoyan'ana zaunduna wa zachitetezo;
 - Agwile nchito kwa zaka zosapambana zisanu ndi kuwonjezedwa kamodzi;
 - Kutsogolela malinga ndi mfundo zochokela ku nduna yoyan'ana za unduna wa zachitetezo atalamulidwa ndi mtsogoleli wadziko.

4 **Bungwe la Defence Forces Service Commission**

- Asilikali a chitetezo adzatsogoleledwa ndi bungwe la Defence Forces Service Commission.

- Nthambi za bungwe limeneli ziyenela kukhala wopunzila ndikuzindikila zinchito zawo, ndiye akusankhidwa ndi mutsogoleli wadziko.
- Zinchito zake zikuphatikiza:
 - Kukhazikidwa ndi kupititsa mutsogolo kayendesedwe ka nchito;
 - Kukhazikitsa malipilo a nthambi za asilikali;
 - Kukhazikitsa ubale wabwino pakati pa asilikali ndi nzika zonse za boma;
 - Kuweluzaboma pa nkani zokhudza za asilikali a chitetezo.

GAWO 3

Apolisi (219-223)

1 Bungwe la aApolisi

- Lili ndi udindo:
 - Kusungalamulo la dziko, kakhalidwe kabwino ndi chitetezo;
 - Kuteteza anthu ndi katundu wawo.
- Liyenela kukhalila:
 - Logwililana nchito dziko lonse;
 - Kukhalilamumbuyo madziko ndi kukonda dziko;
 - Kukhala wodziwanchito yawo;
 - Wosakondela mbali iliyense;
 - Kukhalilapansi pa mphamvu za omwe sali asilikali.

2 Commissioner-General wa Apolisi

- Commissioner-General wa Apolisi:
 - Amasankhidwa ndi mutsogoleli wa dziko atakambilana ndi nduna yoyan'anila za apolisi;
 - Ayenela kugwila nchito kwa zaka zisanu ndikupitiliza zaka zimenezi kamodzi;

- Sangasankhidwe kutsogolela lina bungwe la za chitetezo;
- Amatsogolela malinga ndi mfundo zokhazikidwa ndi nduna yoyan'ana bungwe la apolisi ndunayi italoledwa ndi mutsogoleli wadziko.

3 Bungwe la Police Service Commission

- Apolisi adzalamulidwa ndi bungwe la Police Service Commission.
- Nthambi za bungweli ziyenela kukhala anthu odziwa nchito, wopunzila ndipo asankhidwa ndi mutsogoleli wa dziko.
- Nchito zabungwe ili ziphatikiza:
 - Kukhazikitsa za kayendesedwe ka nchito;
 - Kukhazikitsa za malipilo;

a nthambi za bungwe la apolisi;

- Kukhazikitsa ubale wabwino pakathi pa apolisi ndi anthu wamba, nzika za dziko;
- Kuweluzaboma pankani za apolisi.

GAWO 4

Apolisi a chinsinsi (Ndime 224-226)

1 Nthambi ya Intelligence

- Nthambi ya intelligence iyenela kukhazikitsidwa mwalinga ndi lamulo lalikhulu ladziko, kapena kusankidwa ndi mutsogoleli wadziko, kapena nduna zaboma
- Ayenela kukhalila:
 - Kugwilila nchito dziko lonse;
 - Wokhalila mumbuyo mwa dziko;
 - Wodziwa nchito yawo;
 - Wosakondela kumbali iliyense;
 - Kudziyika pansipamphamvu za omwe sali wogwila nchito kumabungwe achitetezo.

2 Utsogoleli

Mutsogoleli wa nthambi ya Intelligence Services:

- Amasankhidwa ndi mutsogoleli wadziko;
- Kugwila nchito kwa zaka zisanu ndipo akhoza kupitiliza kamodzi chabe;
- Sangasankhidwe kutsogolela lina bungwe la chitetezo;
- Kutsogolela malinga ndi mfundo za nduna yoyan'ana nchito za apolisi a chinsinsi palolezo la mutsogoleli wadziko.

GAWO 5

NDENDE NDI AKAIID (Ndime 227-231)

1 Nchito ya za ndende

- Nchito yake ndiyo:
 - Teteza dziko kuchokela ku mbala, kuwatsekela ndi kuwapunzitsa;
 - Kutsogolela nchito zokopa akayidi ndikusamalila komwe akukhala.
- Thambi ya prison service iyenela kukhala:
 - Yogwila nchito dziko lonse;
 - Kukhalila pambuyo pa dziko;
 - Kudziwa nchito yawo bwino;
 - Wosakondela kumbali ili yense;
 - Liyenela kubvomeleza mphamvu za omwe sali wogwila nchito zosunga akayidi.

2 Commissioner-General wa Prisons and Correctional Service

- Commissioner-General wa nthambi ya prison:
 - Amasankhidwa ndi mutsogoleli wa dziko pokambilana ndi nduna yoyan'ana nthambi ya Prison Service;

- Amagwila nchito kwa zaka zisanu chabe, koma zikhoza kuwonjezedwa kamodzi ngathi akugwila nchito yake bwino;
- Sangasankhidwe kuti atsogolele lina bungwe la zachitetezo;
- Akutsogolela malinga ndi mfuno za nduna yoyan'anila za ndende ndi kusungidwa kwa akaidi palolezo la mutsogoleli wa dziko

3 Bungwe la Prisons and Correctional Service Commission

- Nchito yakhe idzatsogololedwa ndi bungwe la Prisons and Correctional Service Commission.
- Nthambi za bungwe limeneli ziyenela kukhala zodziwa nchito kukhala zotsogololedwa ndipo kusankhidwa ndi mutsogoleli wadziko.
- Nchito yake ikuphatikiza:
 - Kukhazikidwa kwa kayendesedwe ka nchito;
 - Kukhazikitsa malipilo a wogwila nchito ku nthambi imeneyi;
 - Kukhazikitsa ubale wabwino pakati pa nthambi za bungwe ili ndi nzika zadziko;
 - Kuweluzwa boma pa nkani za chitetezo.

MUTU 12

MABUNGWE ODZIYIMILA PAOKHA OTHANDIZILA ULAMULIRO WACHILUNGAMO

GAWO 1

ZAPADELA (Ndime 232-237)

1 Zofunikila Za Mabungwe Amenewa

- Pali mabungwe asanu oti:
 - La Zimbabwe Electoral Commission;
 - La Zimbabwe Human Rights Commission;
 - La Zimbabwe Gender Commission;

- La Zimbabwe Media Commission;
- La National Peace and Reconciliation Commission.
- Adzagwila nchito yokhalila pambuyo ulamulilo wokomela munthu aliyense:
- Kulemekeza ufulu wa anthu ndi ulamulilo wokomela munthu aliyense;
- Kuteteza ufulu ndi zofuna za nzika za dziko;
- Kukwezeletsedwa kwa kugwilitsidwa nchito kwa lamulo la dziko;
- Kukwezeleza chilungamo ndi kusamalila kumabungwe a boma;
- Kusunga mfundo zokomela munthu ali yense kumabungwe onse;
- Kuona kuti zolakwika zonse zakhonzedwa.
- Adzachitanso izi:
 - Kugwila nchito yawo bwino mosatsatidwa ndiponso popanda mantha, mosasankhula, kapena kulowelela kwa ena;
 - Koma kuvomela ndi kuyankha kunyumba ya malamulo pakagwilidwe ka nchito;
 - Kutetezedwa ndikukhalidwa mmbuyo ndi boma pakusungidwa kwa ufulu wawo.

2 **Nthambi Za Mabungwe Amenewa**

- Nthambi za mabunggewa zimasankhidwa ndi mutsogoleli wadziko ndi thandizo la nyumba ya malamulo ndi anthu.
- Nthawi yawo panchito ndi yotetezekha.
- Nthambi ziyenela:
- Kugwila nchito malinga ndi lamulo la dziko;
- Kugwila nchito yawo mosakondelela mbali ili yonse;
- Sayenela kulowelela mu nkani za ndale;
- Wasasokoneza ufulu wofunikila ndi kumasuka kwa nzika za dziko.

GAWO 2

Bungwe la Electoral Commission (Ndime 238-241)

1 Nthambi Za Bungwe La Electoral Commission

- Wapampando pa Bungweli, ndi munthu otha kuweluza milandu, wogwila nchito ngathi woweluza milandu chakhale kapena munthu wokhala ndi zonse zofunikila pa nchito ya woweluza milandu, amasankhidwa ndi mutsogoleli wadziko mokhambilana ndi bungwe la Judicial Service Commission ndi thandizo la nyumba yamalamulo ndi anthu.
- Nthambi zina zisanu ndi zitatu (8) zisankhidwa ndi mutsogoleli wadziko ndi thandizo la nyumba yamalamulo ndi anthu.
- Ayenela kukhala nzika yadziko.
- Ayenela kukhala anthu a ulemu.
- Ayenela kugwila nchito kwa zaka zisanu ndi chimodzi (6yrs) zomwe akhoza kupitiliza nchito yake kamodzi ndi zina zaka zisanu ndi chimodzi (6years).

2 Nchito Za Bungwe ili

- Ndi kutsogolela za kayendesedwe ka masankho ofuna mutsogoleli wadziko, azigawo, kumakosolo ndi chisankho cha mfumu zadziko pamodzi ndi zisankho za referendum, kuphatikizapo:
 - Kulembetsa anthu omwe adzaponye chisankho;
 - Kukhazikitsa kaundula wa mayina a nthu oponya masankho;
 - Kugamula malile a malo osiyana-siyana;
 - Kuphunzitsa anthu kuponye mavoti;
 - Kukhazikitsa madandaulo;
 - Kupatsila malipoti okhudza za chisankho chili chonse mofulumila. (Ndime 238-241)

GAWO 3

Bungwe la Human Rights Commission (Ndime 242-244)

1 Nthambi za bungwe la Human Rights Commission

- Wapampando, yemwe ndi woweluzza milandu, yemwe anagwila nchito ngathi woweluzza milandu kapena munthu woyenela kusankhidwa ngathi woweluzza milandu, akusankhidwa ndi mutsogoleli wadziko atakambilana ndi bungwe la Judicial Service Commission pa thandizo la nyumba yamalamulo ndi anthu.
- Zina zisanu ndi atatu akusankhidwa ndi mutsogoleli wadziko ndi thandizo la nyumba yamalamulo ndi anthu.
- Ayenela kukhala anthu olemekizeka.

2 Nchito ya bungwe limeneli

➤ Udindo wake ndiwo:

- Kukwezeleza ndi kufalitsa uthenga wokhudza za ufulu wa anthu mudziko lonse;
- Kuyan'anila zokutsatidwa kwa ufulu wa anthu;
- Kulandila madandaulo ndikutetsa madandaulo amenewa ndi njila zoyenela;
- Kuteteza anthu pakusagwilitsidwa bwino nchito mphamvu ndi boma, ndi mabungwe a boma pamodzi ndi wogwila nchito muboma;
- Kufufuza zakusokonenezedwa kwa ufulu wa anthu;
- Kupeza chilungamo choyenela kwa anthu ochimwidwa;
- Kulangiza mutsogoleli wadziko kuti afufuze nkani zolephela kuyan'anila za ufulu wa anthu;
- Kuchezela ndi kupenyetsetsa kayimidwe ka ndende ndi ena malo komwe anthu amasungidwa akamangidwa;
- Kufuna malipoti kuchokela kumunthu aliyense kapena bungwe pa nkani ya zomwe zikuchitidwa poyan'anila za ufulu wa anthu kapena kupatsila mawu ogwilitsa nchito kukonza malipoti apadziko lonse lapansi;
- Kuyankha ndi kuthula malipoti kunyumba yamalamulo.

GAWO 4

Bungwe la Gender Commission (Ndime 245-247)

1 Nthambi za bungwe la Gender Commission

- Wapampando ndi ena asanu ndi atatu (8) akusankhidwa ndi mutsogoleli wadziko ndi thandizo la nyumba yamalamulo pamodzi ndi anthu.
- Ayenela kukhala anthu wolemekezeka ndi kuzindikila nkani zokhudza za amuna ndi akazi.

2 Nchito ya bungwe limeneli

Lili ndi udindo wo:

- kuyan'anila nkani zakuyanjana pakathi pa amuna ndi azimai;
- kufufuza zakusatsatiliidwa kwa lamulo;
- kukwezeleza zadziwitso yokhudza za ufulu wa anthu mudziko lonse;
- kuyan'anila kasungidwe ka ufulu wa anthu;
- kulandila madandaulo ndikuwalongosola pa njila yofunikila;
- kuweluza anthu ndi mabungwe osiyana-siyana kutsatila njila zoyenela pobwelesa kuyanjana kwa mipata pakati pa amuna ndi azima;
- kuyitanila mfundo ndi maporogaramu oyanjanisa anthu onse ndi kumanga onse wochita zaumbala;
- kulipila milandu yonse yochimwli anthu;
- kupatsila malipiti kunyumba ya malamulo.

GAWO 5

Bungwe la Media Commission (Ndime 248-250)

1 Nthambi za Media Commission

- Wapampando ndi ena asanu ndi atatu (8) akusankhidwa ndi mutsogoleli wadziko ndi thandizo la nyumba yamalamulo pamodzi ndi anthu.

- Ayenela kukhala anthu wolemekezeka ndi kuzindikila nkani zokhudza za kayendesedwe ka nkani mabungwe autolankani.

2 Nchito ya bungwe limeneli

- Lili ndi udindo wo:
- Kukwezeleza kumasulika kwa mabungwe a utola nkani;
- Kukwezeleza kachitidwe koyenela ka nchito zimenezi;
- Kuyan'anila nchito zoulusa pokukondwelesa anthu onse ndi kuonela kuti pali mapepala osiyana-siyana;
- Kuyikapo njila zotsatila kuti pakhazikidwe kapena kuti bungweli likukhazikitsa ndi kutsogolela zoyenela kutsatilidwa ndi atolankani; nkani za mipata yoyanjana pakati pa amuna ndi azimai;
- Kulandila madandaulo ndi kulongosola nkani ngathi atolankani atalakwa nchito yawo;
- Kuona kuti anthu ali yense akupeza mawu ndi uthenga, kukwezeleza mipikisano ndi kuchuluka kwa mabungwe a utolankani;
- Kukwezeleza kugwilitsidwa nchito kwa zilankhulo zozindikilidwa mudziko lino.
- Kupeleka malipoti kunyumba yamalamulo.

GAWO 6

Bungwe laNational Peace and Reconciliation Commission (Ndime 251-253)

1 Nthawi yogwila nchito

- Bungwe limeneli lidzakhala pa nchito kwa zaka khumi mumbuyo mwa kukhazikikitsidwa kwa lamulo limeneli.

2 Nthambi za National Peace and Reconciliation Commission

- Wapampando wa Bungweli, emwe ndi woweluzza milandu, wogwila nchito ngathi woweluzza milandu kale kapena munthu wokhalila ndi zonse zofunikila pa nchito ya woweluzza milandu, amasankhidwa ndi mutsogoleli wadziko atalankani ndi:

bungwe la Judicial Service Commission ndi thandizo la nyumba yamalamulo ndi anthu.

- Wapampando ndi ena asanu ndi atatu(8) akusankhidwa ndi mutsogoleli wadziko ndi thandizo la nyumba yamalamulo pamodzi ndi anthu.
- Ayenela kukhala munthu wolemekezeka, waluso poyanjanisa, kukhulukililana, kulimbikana ndi phokoso ndi utsogoleli wabwino.

3 Zinchito za bungwe limeneli

- Lili ndi udindo wochita zotsatila izi:
- Kuona kuti pali chilungamo mumbuyo maphokoso, kuyanjanitsa anthu pamodzi ndi kukhulukililana;
- Kukonza ndi kukhazikitsa ma njila zobwelesa ubwino, kugwilizana ndi kutetsa kusamvana pa njila ya bata ndi mutendele ndi kuona kuti pali kulankhulana kwa bwino pakati pa anthu onse osamvana;
- Kuona kuti pali zoonapazomwe zinachitika kale munkani zaphokoso ngathi njila yobwelesa kukhulukililana, ndikubwelesa chilungamo;
- Kukhazikitsa zothandiza ndi kuchilitsa onse wobvutisidwa;
- Kukhazikitsa mfundo zoyan'anila njila zoyambitsa phokoso ndi kukangana ndikuletsa zimenezi;
- Kuthandiza kubwelesa mbali zokangana pamodzi kuti zigwilizane;
- Kulandila madandaulo ndikuchita zoyenela pa nkani zimenezi;
- Kupeleka malipoti kunyumba yamalamulo.

MUTU 13

Mabungwe olimbikana ndi ukatangale ndi milandu

GAWO 1

Bungwe la Zimbabwe Anti-Corruption Commission (Ndime 254-257)

1 Nthambi za bungwe la Anti-Corruption Commission

- Wapampando ndi ena asanu ndi atatu(8) akusankhidwa ndi mutsogoleli wadziko ndi thandizo la nyumba yamalamulo pamodzi ndi anthu.
- Ayenela kukhala anthu wolemekezeka ndi kuzindikila nkani zokhudza za kulongoledwa ndi kuyimbidwa kwa milandu.
- Amenewa:
 - Ayenela kuzigwilila nchito yawo okha, popanda mantha, kudalila mbali iliyense, kukakamizidwa kapena kuti pakhale woloweleda pa nchito zawo;
 - Kuyankha kunyumba yamalamulo kuchitila kuti nchito yawo iziyenda bwino;
 - Kuthandizidwa ndi kutetezedwa ndi mabungwe a boma paufulu wa nchito zawo.
- Ali ndi chitetezo panthawi yogwila nchito zawo.

2 Nchito ya bungwe limeneli

- Lili ndi udindo wochita izi:
 - Kufufuza ndi kutulusa poyela utangale kumabungwe a boma ndi oziyimila paokha;
 - Kulimbikana ndi ukatangale, kuba, kusagwilitsidwa bwino kwa mphamvu ndi kena kachitidwe kosayenela;
 - Kukwezeleza zoona, kuyendesa bwino nkani za ndalama ndi chilungamo;
 - Kulandila madandaulo kuchokela ku anthu ndikuchita zoyenela pa nkani zimenezi;
 - Kulondolela Commissioner-General wa apolisi kuti afufuze nkani za ukatangale ndikupatsila zotsatila zake ku bungwe limeneli;

- Kuyika njila zolimbikana ndi ukatangale;
- Kupatsila malipoti kunyumba yamalamulo
- Boma liyenela kuona kuti bungwe limeneli lidzapempha kuti wopezeka ndi milandu amangidwe ndikuyimbidwa milandu.

GAWO 2

Bungwe la National Prosecuting Authority (Ndime 258-263)

1 Za bungwe limeneli

Nchito yake ndiyoyimba milandu, ndipo likutsogolewa ndi Prosecutor- General wokhala ndi luso ngathi la woweluzamilandu kubwalo la Supreme Court.

MUTU 14

Maboma a zigawo ndi apakati (Ndime 264-266)

1 Kugawilidwa kwaMphamvu Zaulamulilo

- Zina zazifukwa zofalitsa mphamvu za boma ndi maudindo zikuphatikiza kupatsa anthu mipata yolamulira nawo dziko, kukhazikitsa utsogoleli wokwanilitsa ali yense, boma loyendesa nchito yake mofulumira, pachilungamo ndi kukhazikitsa boma lobvomela ngathi litalephela nchito yake, kuchita kuti pakhale kugawana moyanjana zipatso, ndikuzindikila ufulu wamadela kutsogolela pakakhalidwe kawo.
- Cholinga chakhe ndi:
 - Kuona kuti anthu kumaboma apakati akutenga nawo mbali popatsila maganizo a zautsogoleli wa boma
 - Kuona kuti madela osiyana-siyana akuzigwilila nchito zawo kumadela amenewa;
 - Kuona kuti pali kugawana koyanjana kwa ziphatso zadziko ndikuona kuti boma pakati lili ndi ndalama zokwanila zogwilisa nchito zawo.

2 Mfundo za maboma akuzigawo ndi apakati

➤ Maboma apakati ayenela:

- Ayenela kugwila nchito yawo bwino mwa ulamulilo wamphamvu ndikugwilizana kwa nthambi zonse za maboma;
- Kuchita zinchito zomwe ayenela kuchita;
- Kuchita zinchito zimenezi kumalo ndi malile awo komwe ali ndi mphamvu;
- Kugwilizana ndi ena maboma kudzela mukambilana, kuyanjanisa zinchito zawo kudzela kunjila zolengezedwa ndi lamulo lotsogolela nchito za maboma apakati;
- Kuwonela kuti palikuyanjana palowa kumaboma amenewa kwa anthu amadela onse omwe akutsogolela.

3 Wogwila Nchito Kumaboma A Kuzigawo Ndi Maboma:

➤ Ayenela:

- Kutsatila lamulo ladziko;
- Asakhale wokondela chipani chandale;
- Akhale osakhudza zandale;
- Kulemekeza ufulu wofunikila wa nzikandi kumasulika kwawo.

GAWO 2

Maboma akuzigawo ndi akumatauni aakulu (Ndime267-273)

1 Zigawo ndi maboma

- ### **➤ Kudzakhala zigawo khumi mudziko zoti:**
- Bulawayo Province;
 - Harare Province;
 - Manicaland Province;
 - Mashonaland Central Province;

- Mashonaland East Province;
- Mashonaland West Province;
- Masvingo Province;
- Matabeleland North Province;
- Matabeleland South Province;

ndi

- Midlands Province.

➤ Kudulidwa kwa maboma kudzachitidwa ndi lamulo ladziko.

2 **Maboma akuzigawo**

➤ Chigawo chili chonse chidzakhala ndi konsolo yopatikiza:

- Anthu onse omwe ali amphungu a nyumba yamalamulo wochokela kuchigawo chimenechi;
- Mameya onse ndi wakumpando wa maboma apakati a chigawo chimenechi;
- Anthu khumi osankhidwa malinga ndi mavoti oponyedwa pa nthawi ya chisankho;
- Wapampando osankhidwa ndi nthambi zolengezedwa pamwamba kuchokhela kusankhidwa ndi chipani chokhalila ndi anthu ochuluka omwe ndi aphungu a nyumba ya National Assembly kuchigawo chimenechi.

3 **Makonsolo akumatauni aakulu**

➤ Konsolo iliyense yakumatauni aakulu imakhala ndi anthu awa:

- Anthu onse omwe ali aphungu anyumba yamalamulo kuchokela kuchigawo chimenecho;
- Mabwanankuba onse ndi wowatsatila ndi apamumpando wa makonsolo onse a chigawo chimenecho;
- KuBulawayo, wapampando kukonsolo ndi emwe adzakhala bwanankuba wa tauni ya Bulawayo;

- Ku Harare, wapampando ku konsolo ya Harare ndiye womutsatila adzakhala bwanankuba kapena wapampando wakonsolo yachiwili pokula kuchigawo chimenecho.

4 Nchito za makonsolo akuzigawo ndi matauni aakulu

- Nchito yawo ikuphatikiza:
 - Kukwezeleza zakakhalidwe ndi chitukuko cha chuma;
 - Kutsata ndi kukhazikitsa nchito za boma;
 - Kusamalidwa kwa zachilengedwe;
 - Kutsogolela pakugwilitsidwa nchito kwa zopezeka zonse.
- Wogwila nchito kumakonsolo adzalembedwa nchitozi malinga ndi lamulo ladziko.
- Makonsolo akuyankha ku anthu a chigawo ndi boma.

5 Wapampando ku zigawo ndi matauni aakulu

- Ayenela kukhala anthu okhoza kusankhidwa ngathi aphungu anyumba yamalamulo.
- Wapampando ku konsolo yakuchigawo adzasankhidwa ndi konsolo ya kuchigawo kuchokela pa anthu ofika awili kapena kupambana kuchokela kuchipani chokhalila ndi mipando yochuluka, kapena wopeza mavoti ochuluka pa chisankho chofuna aphungu a nyumba yamalamulo kuchigawo chimenecho.
- Akhoza kuchotsedwa pa nchito ndi bungwe lokhazikitsidwa koma loziyimila pa lokha atalephela kugwila nchito yawo, atachita zosayenela, atapezeka ndi milandu yakuba, ukatangale kapena kulakwila lamulo ladziko.

GAWO 3

Boma lapakati (Ndime 274-279)

1 Makonsolo akumatauni

- Adzakhala nayan'anila z nkani zakumatauni.
- Adzakhala akutsogoleledwa ndi anthu osankhidwa ndi anthu omwe atsogoleli awo adzakhala ma bwanankuba kapena wapampando.

- Ngati bwanankuba adzafune kukhala bwanankuba wa mphamvu (executive mayor) ayenela kusankhidwa ndi anthu okhala kudela limenelo.

2 Makonsolo akumidzi

- Adzakhala akuyan'anila nchito ndi nkani zakumadela akumidzi.
- Kusankhidwa kwa nthambi za kosolo, wapampaando ndizofunikila zawo zizakhalila malinga ndi lamulo la dziko.

3 Zokhudza makonsolo onse

- Adzakhala ndi mphamvu:
 - Kukhazikitsa malamulo apadela ndi zina zokhudza zakayendesedwe ka nchito kumadela awo;
 - Misonkho ndi malipilo ndi nchito yawonso.
- Masankho amachitidwa pa nthawi imodzi ndi chisankho chamutsogoleli wadziko ndi aphungu.
- Mabwanankuba ndi wapampando, kusiya kwa amene akusankhidwa ndi anthu, adzasankhidwa pamusonkano woyamba wa konsolo.
- Nthambi za makonsolo amataikidwanso ndi zinchito zawo ngathi momwe aphungu anyumba yalamulo, ndiye amachotsedwa pa nchitozi ndi bungwe lapadela liziyimila palokha ngathi atalephela kugwila nchito yawo bwino, atapezeka ndi milandu yakuba, ukatangale kapena kulakwila lamulo ladziko

MUTU 15

Atsogoleli a chikhaliidwe (Ndime 280-287)

1 Kuzindikilidwa

- Mutu umenewu ukuyan'ana nchito ndi utsogoleli palamulo lazakakhalidwe, pakakhalidwe ka mfumu, atsogoleli a makhola ndi ena atsogoleli kumalo omwe akutsogolela.
- Ndi bungwe loziyimila palokha

2 Atsogoleli a zakakhalidwe

- Ayenela:

- Kugwila nchito malinga ndi malamulo adziko;
- Osakondela kumbali ili yense;
- Osadalila kapena kusala anthu pa nkani za ndale;
- Wosasokoneza ufulu wofunikila ndi kumasulikha kwa munthu aliyense;
- Kuyan'anila lamulo la kakhalidwe malinga ndi lamulo ladziko lonse;
- Kugwila anthu onse moyanjana.

➤ **Nchito zawo zikuphatikiza:**

- Kukwezeleza ubwino wa zakakhalidwe, miyambo, ndondomeko ndi zina zabwino za madela komwe amakhala;
- Kukwezeleza ubwino wa mabanja;
- Kupititsa mutsogolo nchito za chitukuko;
- Kuthetsa nkani zochimwilana pakati pa anthu malinga ndi lamulo la zakakhalidwe.

➤ Amakhazikitsidwa ndikuyimitsidwa nchito:

- ndi mutsogoleli wadziko;
- Malinga ndi lamulo ndi miyambo yakumadela kwawo;
- Kuchokela pamawu a mfumu za konsolo za bungwe Provincial Council of Chiefs ndi nduna ;
- Popanda kuyan'ana pa nkani za ndale.

➤ Malipilo awo amakhazikidwa ndi lamulo ndichilolezo cha mutsogoleli wadziko.

3 Konsolo ya dziko lonse ndi mabungwe a mfumu

- Mabungwe a National Council of Chiefs ndi bungwe la mfumu kudzakhala malinga ndi lamulo ladziko.
- Bungwe la National Council of Chiefs limayimila mfumu zonse zadziko la Zimbabwe. Bungwe la Provincial Councils of Chiefs limayimila mfumu zonse zachigawo chimenecho kusiya kwa chigawo chakumatauni.

- Kusankhidwa kwa mfumu kukhala kubungwe la National Council kudzakhala malinga ndi lamulo ladziko akuyimila zigawo zosiyana-siyana.
- Mabungwe a Provincial Assemblies amasankha mfumu zokhalanso kunyumba ya senate.
- Nchito zawo zikuphatikiza:
 - Kukwezeleza ndi kuteteza kakhaliidwe ka anthu ndi miyambo yawo;
 - Kuyimila maganizo a atsogoleli a za chikhalidwe ndikupititsa mutsogolo zofuna zawo;
 - Kukhazikitsa ndi kutulusa poyela kakhaliidwe koyenela.

4 Komiti yolongosola za kakhaliidwe

Komiti yolongosola za kakhaliidwe ka mfumu idzakhazikidwa ndi lamulo kuti ibweletse kakhaliidwe kaulemu ndi kuzigwila kwa bwino kwa mfumu, ndikukhazikitsa nkani pakati pa mfumu ndi madandaulo kwa mfumu.

MUTU 16

Nthaka ya zaulimi (288-297)

1 Mfundo zokhudza nthaka ya zaulimi.

- Nzika zonse wosayan'ana mutundu, ali ndi ufulu, kukhala, kugwilitsa nchito kapena kugulitsa nthaka yakhe yazaulimi.
- Kugawilidwa kwanthaka kuyenela kukhala kwachilungamo kokwanila ali yense:
 - Nzika ili yonse yadziko la Zimbabwe ili ndi ufulu woipeza, kusunga, kukhala ndikugwilitsa nchito nthaka ya zaulimi.
 - Ndi nthaka yamuyaya yomwe aliyense ndi mwini;
 - Kuyanjana kwa mipata pakati pa amuna ndi akazi;
 - Kusiyana kwa zofuna kumadela.
 - Nthaka ya zaulimi iyenela kuthandiza dziko kupeza chakudya, ndipo palibe munthu yemwe angalandidwe nthaka yomwe akufuna kugwilisa nchito zaulimi.

- Ufulu wogwilisa nchito nthaka sinkani yopitisa kubwalo lamilandu.

2 Ufulu womwe ulipo pakali pano pa nkani za nthaka

- Boma ndiye mwini wa nthaka yomwe inatengedwa pa nthawi yakugawidwa kwa nthaka ndiye zimenezi zinatsimizikidwa kale.
- Malipilo pa nthaka yotengedwa ndi boma adzakhala kupela pa nthaka:
 - Yotengedwa kuchokela ku nzika zadziko la Zimbabwe ; ndi
 - Yotetezedwa pa chigwilizano pakati pa boma ladziko lino ndi ena mayiko;
- Ufulu ndi uweni pa nthaka yopatsidwa kwa anthu kuti agwile nchito zaulumi ukuzindikilidwa.

3 Ufulu wa nthawi

- Payenela kukhala mfundo zopatsila chitetezo pakugawidwa kwa nthaka yopatsidwa anthu kuti agwilitse nchito zaulimi.
- Boma likhoza kusintha uweni kapena kupatsila kwa wina munthu pamalipilo kapena yina njila pauweni wa nthaka.
- Weni wa nthaka akhoza kupatsila nthaka imeneyi kwa wina munthu.

4 Bungwe la Land Commission

- Mamembala ake akusankhidwa ndi mutsogoleli wadziko.
- Ali ndi chitetezo panthawi yopatsilidwa nthaka imeneyi.
- Nchito yaku ikuphatikizako:
 - Kuona kuti pali ubwino ndi chilungamo potsogolela nkani zokhudza nthaka ya zaulimi;
 - Kuyan'anidwa nthawi ndi nthawi;
 - Kukwanilitsa zofunikila pa mitunda wa minda womwe munthu kapena banja lingakhale nawo;
 - Nkani zonse zakayendesedwe kautsogoleli wa nchito za nthaka ya zaulimi, kupatsila anthu minda, kugwilisidwa nchito kwa minda, mitunda ya minday, zakutengedwa kwa minda ndi boma ndi zina;

- Kukhazikitsa njila zosabvuta pa zakayendesedwe ka nthaka.

MUTU 17

Zachuma (sections 298-317)

1 Kasungidwe ka chuma

- Posunga chuma cha boma:
- Mfundo zoyenela kutsogolela kagwilitsidwe ka chuma chaboma zikuphatikiza chilungamo, kugawidwa kwa zipatso zamudziko moyanjana pakati pa mibadwe ya lelo ndi yamawa, ndi kugwilitsidwa bwino kwa ndalama zaboma panjila zoyenela.
- Kasungidwe ka chuma kayenela kuchitidwa pachitukuko cha dziko;
- Kulipilidwa kwa misonkho kuyenela kuchitidwa moyanjana kwa anthu onse;
- Zopezeka zonse za boma ziyenela kugawidwa moyanjana kuzigawo zonse zadziko kuphatikiza maboma apakati.
- Mavuto ndi mphoto yazipatso za dziko ziyenela kugawidwa moyanjana pakhati pa mibadwe yalelo ndi yamawa;
- Malipoti okhudza za chuma chadziko ayenela kulembedwa ndikutulutsidwa bwino;
- Kutenga ngongole kuyenela kuchitidwa bwino pachilungamo ndiye kukhala kokomela dziko lonse.

2 Kuphonya kwa nyumba yamalamulo

- Nyumba yamalamulo iyenela kuyan'ana kagwilitsidwa nchito kwa ndalama za boma.
- Malile akutenga ndalama za ngongole za boma, ngongole za boma siziyenela kuchitidwa popanda chilolezo cha nyumba yamalamulo.
- Nyumba yamalamulo iyenela kuuzidwa nkani zonse zokhudza ngongole za boma ndi njila zake zobwezela ngongole zimenezi.

3 Kugawilidwa kwa ndalama za boma

- Kugawilidwa kwa ndalama za boma kuyenela kuchitidwa mwoyanjana kumakonsolo onse akuzigawo ndi akumatauni ndi akumidzi mozindikila izi:
- Zofuna zadziko;

- M fundo zoyenela pangongole za dziko;
- Zofuna za boma;
- Zofuna za madela opanda chitukuko chokwanila.
- Kuyenela kwa makonsolo akuzigawo ndi makonsolo akumatauni
- Kusiyanana kwa za chuma kwa zigawo
- Chigawo zisanu muzana (5%) cha ndalama zonse za boma ziyenela kupita ku makonsolo azigawo ndi matauni.

4 Thumba la ndalama la Consolidated Revenue Fund

- Ndalama zonse za boma kuchokela kulikonse ziyenela kuyikidwa muthumba landalama za boma lochedwa Consolidated Revenue Fund.
- Palibe ndalama zololedwa kutuluka muthumba limeneli, koma pokapokapo ngati alikulipila zolamulidwa, ndipo ndalama zonse zotulutsidwa muthumbali ziyenela kupita ku munthu yemwe akuyenela kupatsidwa ndalama zimenezi
- Chaka ndi chaka nduna yoyan'anila za chuma iyenela kupatsila kunyumba yamalamulo dongosolo yakagwilisidwe ka nchito ya ndalama zaboma ndizoyan'anila moganzila kuzigawo za boma muchaka chotsathila
- Ngathi ndalamazi zikhalephela kukwanilitsa zinchito zaboma, nduna yoyan'anila zachuma iyenela kuyitanila kuthi pak hazikitsidwe lina dongosolo landalama yapadela lomwe lidzatulutsidwa kunyumba yamalamulo.
- Ngathi ndalama zambili kuposa zolengezedwa zinagwilitsidwa nchito, kapena kuti ndalama zinagwilitsidwa nchito pa nchito yosayenela, nduna yazachuma iyenela kuyitanila munyumba yamalamulo ganizo munyumba yapansi kuthi nyumbayi ilandile kagwilitsidwe kanchito kandalamazi popanda lolezo la boma.
- Lolezo ya lamulo la nyumba yamalamulo likhoza kugwilitsidwa nchito pofuna kuloleza ndalama zogwilitsidwa nchito popanda chilolezo.

5 Ndalama za boma ndi katundu

- ndalama za boma ziyenela kusungidwa bwino ndi katundu wake malinga ndi zobvomelezedwa ndi boma, osati kuzigwilisa nchito panjila yomwe idzachite kuti katundu awonongeke.
- Zilando zoyenela ziyenela kupatsidwa kwa aliyense emwe adzasokoneze ndalama za boma kuti ndalamazi zipezeke.

6 Woyan'anila za mabuku a ndalama ndi katundu wa boma

- Nchito imeneyi ndi nchito yoziyimila pa yokha.
- Nchito ya Auditor-General ndiyo:
- Yan'anila za ndalama ndi mabuku a ndalama ya boma, kutsogoleledwa kwa kagwilisidwe nchito ka ndalama ndi katundu wa boma ku nthambi zonse zaboma;
- Kuyan'anila zakayendesedwe ka nchito za ndalama kumakampani otsogoleledwa ndi boma;
- Kuloleza zakusayenela kwa kutsogoleledwa kwa ndalama za boma.
- Auditor-General amasankhidwa ndi mutsogoleli wadziko pabvomelezo la nyumba yamalamulo.
- Ayenela kukhala nzika ya dziko.
- Amakhala pa nchito zaka zisanu ndi chimodzi (6yrs) ndipo sayenela kukhala pa nchito imeneyi zaka zopambana khumi ndi ziwili(12yrs).
- Malipilo ake akhazikidwa ndi nyumba yamalamulo ndi bvomelezo ya mutsogoleli wadziko.
- Kuchotsedwa kwake pa nchito kuchitidwa ndi mutsogoleli wadziko ndi thandizo la bungwe lokhazikitsidwa kuthi liyan'ane nkani yakuchotsedwa kwake pa nchito.

Za zinchito za onsewe za ku ofesi ya Auditor-General zikukhazikitsidwa ndi bungwe lokhazikitsidwa kuthi ligwile nchito imeneyi.

Kupezeka kwa zinthu za boma

Kupezeka kwa zinthu zonse za boma kudzachitidwa pa lamulo.

8 Mabungwe a zamalamulo

- Payenela kukhala lamulo lokonzedwa munyumba yamalamulo lolengeza kuthi atsogoleli a mabungwe okhazikitsidwa palamulo ladziko adzipatsidwa malile anthawi yomwe ayenela kugwila nchito kumabungwewa.

9 Banki yaikulu yadziko

Pali banki lalikulu la dziko la Reserve Bank of Zimbabwe, yomwe nchito yake ikuphatikiza kuyan'anila zakaendesedwe ka nchito za ndalama, kuteteza ndalama ya dziko za Zimbabwe, ndikukonza pamodzi ndi kukazikitsa mfundo zokhudza zakayendesedwe ka ndalama.

MUTU 18

Zina ndi zothandizila zapadela

GAWO 1

Dongosolo yapadela kumabungwe (Ndime 318-323)

1 Mabungwe osiyana-siyana

- Mabungwe onse:
- Ali ndi kayimidwe ka kampani yaboma;
- Ndi mamembala a mabungwe oziyimila paokha oti Judicial Service Commission, Anti-Corruption Commission ndi Land Commission omwe akupatsidwa chitetezo cha nthawi, koma ena onse amagwila nchito pachifunilo cha mutsogoleli wadziko;
- Wapampando ndi wotsatila wapampando ayenela kukhala anthu osiyana paumuna ndi mukazi;
- Malipilo a anthu ogwila nchito kumabungwe amenewa amakhazikitsidwa ndi lamulo, ndipo sadzachepetsedwa pa nthawi yomwe ali pa nchito;
- Nyumba yalamamulo iyenela kupatsila ndalama zokwanila kuti mabungwe amenewa agwile nchito yawo bwino;
- Ayenela kupatsila malipoti kunyumba yalamamulo.

GAWO 2

Zapadela (Ndime 324-329)

1 Zapadela

- Zofunikila malinga ndi lamulo ladziko ziyenela kuchitidwa bwino.
- Mabungwe okhazikitsidwa palamulo ayenela kupatsidwa ndalama mokwanila.

- Lamulo lapadziko lonse lapansi ndi lamulo ladziko la Zimbabwe ngathi lili malinga ndi lamulo lalikulu la dziko la Zimbabwe.
- Zigwilizano zapadziko lapansi zolembedwa ndi dziko la Zimbabwe ndikulandilidwa ndi nyumba yalamamulo zidzakhalsano mbali ya lamulo la dziko ngathi nyumba yalamamulo italengeza. Chilolezo chidzachokela kunyumba yalamamulo, kusiya kwa zigwilizano zofuna chitsimikizo cha boma kapena ndalama za boma kapena kusintha lamulo ladziko la Zimbabwe.
- Zigwilizano zapadziko lonse lapansi ziyenela kuvomezedwa ndi nyumba yalamamulo.
- Mabwalo amilandu ayenela kumasulila ndikulongsola malamulo omwe akugwilizana ndi zigwilizano zapadziko lonse lapansi ndi zina.

2 **Kukonzedwa kwa lamulo ladziko**

- Masiku makumi asanu ndi anai (90) akufunika kupatsa chidziwitso mu malemba a boma kuchokela ku muneneli wa nyumba yalamamulo kulengeza kuti akufuna kusintha lamulo ladziko.
- Anthu ayenela kuyikapo ndemanga zawo, ndiye misonkano iyenela kuchitidwa pa nkani imeneyi.
- Lamuloli liyenela kulandilidwa ndi mphambu ziwili za aphungu a nyumba yalamamulo iliyense pa nyumba ziwili.
- Kusintha palamulo lokhudza za ufulu ndi kumasulika kwa anthu pamodzi ndi za nthaka kuyenela kuchitidwa ndi chisankho cha referendum (MITU 4 ndi 16) mukati mwa mwezi itatu italandilidwa ndi nyumba yalamamulo. Lidzakhala lamulo ngati litalandilidwa pa chisankho cha referendum.
- Kusintha kwa nthawi yowonjezedwa sikuthandauza kuti kuwonjezela nthawi ya munthu aliyense yokhala pa nchito kusinthaku kusanachitidwe.
- Ndimbe za (6) ndi (7) za ndime zazikulu za 328 za lamulo limeneli sizingakonzedwe pa dongosolo yalamulo imodzi, ndiyenso kusinthidwa kwa ndime zimenezi sikungachitidwe pa referendum imodzi.
- Kukonzetsedwa kwa ndime 328 kwa lamuloli kuyenela kulandilidwa ndi chisankho cha referendum, ndibvomelozo ya mphambu ziwili pa mphambu zitatu za nyumba yalamamulo mukati mwa mwezi itatu nyumba yalamamulo italandila.

3 **Kuyamba kugwila nchito kwa lamulo limeneli**

Lamulo limeneli lidzayamba kugwila nchito muzigawo zosiyana-siyana:

- Chigawo choyamba: patsiku lakulengezedwa kwa lamulo limeneli zotsathila zi zidzayamba kugwila nchito:
- Mfundo zololeza chisankho choyamba palamulo latsopanoli ndipo zimenezi zikuphatikiza:
- Mutu wokhudza za zisankho;
- Chisankho cha mutsogoleli wadziko (kusiya kwa kuti mutsogoleli wadzikoyu, mukati mazaka khumi zadzasankha anthu wogwilizana naye pa nthawi yachisankho, koma kuti adzasankha wotsatila mutsogoleli wadziko, ndiye ngathi padzakhale kuti mpando wa mutsogoleli wadziko woyamba wakhala ulibe munthu, wina kuchokela kuchipani chake adzasankhidwa(yan'anani pa ndime 14 ya lamulo limeneli).
- Mutu wokhudza za aphungu anyumba yalamamulo ndi kuyitanidwa kwa nyumba yalamamulo;
- Mutu pa mfundo zakayendesedwe ka nchito za boma ndi utsogoleli;
- Mfundo zokhuza kayendetsedwe ka nchito ya chitetezo;
- Mfundo zokhudza kuyan'anila za masankho kubungwe la Electoral Supervisory Commission
- Mutu pa nkani za ufulu ndi kumasulika;
- Mfundo zokhudza bwalo la malamulo a dziko;
- Mutu pa nkani zokhudza maboma azigawo ndi makonsolo.

Mfundo zimenezi zidzapambana kuyanjana kwa mfundo zoyanjana lamulo latsopanoli

- Chigawo chachiwili: tsiku lomwe mutsogoleli wadziko adzatenge mpando wake, zonse za lamulo limeneli zidzayamba kugwila nchito.

Ndime ya 329 idzakhala ikugwila nchito limodzi ndi gawo lachisanu ndi limodzi (6th)

GAWO 3

Masulilo (Ndime 330-345)

- Mundime imeneyi, mawu ogwilitsidwa nchito mulamulo limeneli akupezeka pa ndime 322.

- Zina nkani zikulongoseledwa mu ndime imeneyi, pakati pazina ndi:
 - zothandauzila:
 - “kuchita pabvomelezo ya” kunena kuti mphamvu zomwe zikuzidwa ziyenela kutsatila zomwe auzidwa;
 - Kuchita “mbuyo mokambilana ndi...” zikuthandauza kuti mphamvu zoyenelazo ziyenela kugwilizana ndi, koma sayenela kutsata mfundo zokhazikidwa;
 - Kusiyazinchito:
 - Mutsogoleli wadziko amasiya nchito ndikuuza muneneli wanyumba yalamamulo;
 - Muneneli wa nyumba yalamamulo ndi mutsogoleli wa nyumba ya Senate ndi wowatsatila, atapatsila nkaniyi kumulembi wa nyumba yalamamulo, kapena ndikulengeza kunyumba yalamamulo yoyenela;
 - Aphungu anyumba yalamamulo, kudzela mukupatsila chidziwitso ku muneneli wanyumba yalamamulo kapena mutsogoleli wa nyumba ya Senate, malinga ndi zofunikila;
 - Nthambi za mabungwe okhudza za malamulo, kupita ku bungwe lokhazikitsa;
 - Unyinji wa anthu wofunikila kukhalila chili chonse:
 - Kawili-kawili, chigawo chapakati cha nthambi za bungwe lokhudza zamalamulo ndiomwe akukhazikitsa unyinji wa anthu wofunikila kuti chili chonse chichitike;
 - Kusoweka kwa wina munthu wogwila nchito kubungwe lililonse sikungayimitse nchito ngathi pali unyinji wa anthu wofunikila kuchita chisonkano;
 - Chiwelengelo chanthambi zonse zanyumba yalamamulo kumapathula mipando yopanda anthu.